

YEHOVA-YIRE ³



Tiweramitse mitu yathu mphindi yokha kwa pemphero.

Ndipo iye anatcha dzina la malowo Yehova-yire: monga momwe ziriri...kuwoneka...Mu phiri la AMBUYE mpaka...tsiku lino.

² Atate athu Akumwamba, ife tiri oyamikira usikuuno kukhala ndi mwayi uwu wa kusonkhana limodzi mu Dzina la Ambuye Yesu, kumupembedza Iye mu Mzimu wa chiwukitsiro Chake. Ndipo ndife oyamikira kwambiri kwa Inu, chifukwa cha zomwe Inu mwatichitira kale ife, pozidzindikiritsa Nokha mwa Mawu pakati pathu, ndi mwa chiukitsiro. Ndipo ziyembekezo zathu zamangidwa pamwamba kwambiri, Ambuye, chifukwa ife tikudziwa kuti—kuti Mulungu amene ife tikumutumikira si mulungu wina wa mbiriyakale, koma Mulungu wanthawi ino, Amene anaukitsidwa kwa akufa, ndipo watsimikizira kuti ali Mulungu yemwe anali ndi Mose, ndi Abraham, ndi atumwi onse, ndipo akadali Mulungu yemweyo. Ndiye wathu...Ife tikulumikizana ndi Eddie Perronet, monga iye ananena, “Ziyembekezo zanga sizinamangidwe pa china chirichonse koma Magazi a Yesu ndi chirungamo.” Koteru, ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha chithonhozo chachikulu ichi ndi chithonhozo chimene ife tiri nacho.

³ Atate, usikuuno, ngati alipo mmodzi pano pakati pathu, usikuuno, amene alibe chiyembekezo chachikulu ichi, mulole ili likhale ora limene Choonadi chimodzi chachikulu Chamuyaya chiti chidzawululidwe kwa iwo, Atate, kuti iwo adzadziwe kuti chifukwa chimene iwo anabwerera kuno pa dziko lapansi si basi kuti—kuti adzagwire ntchito. Ndipo ndicho chimodzi mwa zifukwa, ndithudi. Koma chifukwa chachikulu ndikudzakhala mwana wamwamuna kapena wamkazi wa Mulungu. Ndipo mulole izo zitsirizike, usikuuno. Perekani izi, Ambuye.

⁴ Tidalitseni ife tsopano pamene ife tikuyanjana pozungulira Mawu Anu. Mawu Anu ndi Choonadi. Ndipo mulole Mzimu Woyera wawukulu uwatenge Mawu a Mulungu ndi kuwagawa Iwo kwa ife monga ife tikuwasowa, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Mukhoza kukhala pansu.

⁵ Zikomo inu chifukwa cha mwayi wobweranso kachiwiri usikuuno, ndi kudzakumananso ndi inu anthu abwino ndi Uthenga wa ulemero uwu. Ife talengeza kuti, tsopano, mawa mmawa Sande sukulu, azibusa olumikizana ndi ogwirizana adzakhala ndi Sande sukulu yolumikizana pomwe pano. Ine ndikuganiza kuti zimenezo ndi zabwino kwambiri. Ndipo ambiri a iwo atenga mipando kuchokera mmatchalitchi awo

ndipo ayibweretsera iyo kuno chifukwa cha anthu, ndipo iyo ndithudi ndi ntchito yabwino yokhulupirika kuti anthu achite chinthucho.

⁶ Ndife othokoza kwa Mulungu chifukwa cha nyengo yabwino imene Iye watipatsa ife. Iwo analosera kuti ife tikhala ndi mikuntho ndi zinthu, nthawi zonse. Koma Iye waibweza mikunthoyo, ndipo ife sitinakhale ndi vuto limodzi. Ndife oyamikira chifukwa cha zimenezo.

⁷ Ndipo tsopano, usikuuno chinaperekedwa...Ife takhala tikungokhala ndi misonkhano yachizolowezi ya ulaliki. Ndipo ngati pali alendo aliwonse ali nafe...Ife sitinatsindike kwambiri pa—pa ochimwa akubwera kwa Khristu. Ndipo ndinatenga mutu Lachinayi lapitalo usiku, ndipo ine sindinafike kwa iwo panobe. Ife tikungoyankhula za Abraham, ndipo ife sitinafike ku mutu panobe, wa *Yehova-Yire*. Kotero ife tikuyesetsa kuti titsirize izo usikuuno. Ndipo ife tikudalira kuti Ambuye apulumutsa munthu aliyense wosapulumsidwa, ndi kumudzadza aliyense yemwe sanadzazidwe ndi Mzimu Woyera, usikuuno.

⁸ Tsopano taganizani za zimenezo mwatcheru kwenikweni pamene ife tiri apa. Ndipo pamene ife tiri—pamene ife tikuyankhula, tsegulani mtima wanu kuti Mzimu Woyera uyankhule mkati mwanu. Kodi ife tikuchita chiyani pano, mulimonse? Tangoganiziraninso zimenezo. Kodi, moyo wanu wakhala uli chiyani? Kodi inu mwadzera chiyani pano? Ndi Mulungu...Kodi inu muli mu chikhalidwe chotero kuti Mulungu akhoza kutenga zonse—zonse zimene Iye anakuikirani inu pano, kuchokera mwa inu? Ngati sichoncho, ndiye tiyeni tizikhazikitse zimenezo usikuuno, abwenzi. Ndi a...

⁹ Ine—ine ndiri ndi abwenzi ena amene akhala pano, ochokera ku mpingo wanga. Ena a...Mmodzi wa matrasti, ine ndikudziwa, ndi awiri kapena atatu a abalewo. Ine ndangozindikira kumene banja latsopano lakhala pano, usikuuno, la a Palmer ochokera kuno kwinakwake, amayendetsa mailosi mahandiredi angapo lililonse—Lamlungu lililonse limene ine ndimayankhula uko ku Indiana. Ndipo Bambo Welch Evans ndi banja lawo ali pano penapake. Ine sindikudziwa basi pomwe. Ine...Lero, ine ndakhala ndikuphunzira, pafupifupi tsiku lonse, ndipo ndimakhoza kumva mawu awo kunjani uko. Ndipo ine—ine ndinadziwa iwo ali pompano.

¹⁰ Tsopano, mawa, mawa pa thuu. [Wina akuti, “Thuu.”—Mkonzi]. Pa thuu koloko, mawa, msonkhano wonse mawa madzulo udzaperekedwa kwa odwala, kwa pemphero la odwala. Tsopano, anthu ambiri amazitcha izo ngati msonkhano wa machiritso. Chabwino, ife sitimakonda kwenikweni kutchula izo monga chomwecho. Chifukwa, tiyeni tiwutche iwo utumiki wa chikhulupiriro. Kotero, ngati chikhulupiriro chathu

chingakhoze kufika pa malo amenewo, Iye atazindikiritsidwa pakati pathu, ndi kudziwa chirichonse chimene chiri mu mtima mwathu, ndipo watsimikizira izo kwa ife, mwaona, kuti Iye ali wamoyo, ndipo watsimikizira izo mwa Lemba.

¹¹ Kodi inu munazindikira momwe Iye anawayikira kumbuyo Mawu aliwonse, ndi Kukhalapo Kwake kwamoyo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Mukuona? Mukuona? Mukuona? Tsopano, izo zikusonyeza kuti inu simuyenera kungoganiza kuti ife tikungoyesera kunena chinachake chomwe chiri mtundu wina wa nthano inayake. Chimene Baibulo ili lalonjeza, ndicho Choonadi. Mukuona? Tsopano Mawu aliwonse ndi owona.

¹² Tsopano, ine mwina ndikhoza kusakhala ndi chikhulupiriro chokwanira kuti ndipangitse Mawu aliwonse a Iwo kuchitika, koma ndithudi sindingaimo monga aliyense amene anali ndi chikhulupiriro chimenecho. Enoki anali ndi chikhulupiriro chokwanira, tsiku lina, kuti ayende masana ndi Mulungu, ndipo anangopitirira kumayenda, anapita Kwawo wopanda kufa. Tsopano, ine ndikuganiza Mpingo uyenera kubwera ku zimenezo, ku chikhulupiriro Chokwatulitsa. Ine mwina ndikhoza kusakhala nacho chikhulupiriro chimenecho pakali pano, koma ndithudi ine sindingati ndiyime mu njira ya winawake yemwe anali nacho chikhulupiriro chimenecho.

¹³ Kotero, ife tikudalira kuti Mulungu atipatsa ife chikhulupiriro chachikulu, ndipo, mawa kuti sipadzakhala munthu wofooka wotsalira mchipinda muno, pamene iwo azidzadutsa kufuna pemphero. Ife tidzangokhulupirira zimenezo. Ndipo tsopano ngati tidzakhulupirire zimenezo! Tsopano, ine ndaziwonapo zimenezo nthawi zambiri!

¹⁴ Ine ndawonapo nthawi imene twente-faivi sauzande, tangoganizani tsopano, osati twente-faivi handiredi, machiritso opambana twente-faivi sauzande akuchitika ndi pemphero limodzi: Durban, South Africa. Iwo anyanyamula, ine sindikudziwa kuti ndi ma vani aakulu angati, omwe inu... Awiri a iwo akanakhoza kudzaza chinthu chonsechi *muno*, kutenga zimene zinayikidwa mmenemo, galimoto yayikulu yaku Britain, magudumu sikisi ndi eyiti pa iwo, monga choncho, basi vani pambuyo pa vani, akubwera kumeneko, ndi zibonga ndi zikuku, kapena zomwe iwo amazitcha zikuku, tinthu tating’ono timene iwo amanyamulira nato odwala. Ndi kuwabweretsa iwo kudutsa mu nkhalango. Ndipo mkango nkumawatsatira iwo, iwo nkuwakwezera iwo mu mtengo. Ndipo akatero nkumabwerabe ku msonkhano. Ndiyeno kungowona basi, pa nsanja, mnyamata.

¹⁵ Woyamba amene anabwera pa nsanja anali a—analii mkazi. Ndipo iye anyayikidwa chizindikiro Muhamadi, ali ndi dontho lofiira pakati pa maso ake. Ndipo ine ndinamufunsa iye ngati amayankhula Chingerezi. Ndipo iye anati, “Pang’ono chabe.”

Ndipo ine ndinati, “Ine ndikuwona inu ndinu wa Chimuhamedi, wa Chimuhamedi.”

Iye anati, “Inde.”

16 Ine ndinati, “Inu mwabwererANJI kwa ine, ngati Mkhristu? Bwanji inu osapita kwa wansembe wanu?”

Iye anati, “Ine ndikukhulupirira kuti inu mukhoza kundithandiza ine.”

17 Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine sindingakhoze kukuthandizani inu, kupatula, inu mutakhulupirira pa Yesu Khristu.”

Ndipo iye anati, “Chabwino, ine ndaiwona misonkhanoyi.”

18 Basi uko masiku atatu okha. Ife tinali nawo pafupifupi, pafupifupi thuu handiredi sauzande atakhala pamenepo, pa malopo. Koteri ndiye anali atawatchingira iwo, chifukwa iwo anali ali ndi nkondo za mafuko, nawonso.

19 Ndipo ine ndinati, “Chabwino, tsopano, inu muyenera kukhulupirira pa Yesu Khristu.” Ndipo ine ndinati, “Kodi inu munayamba mwawerengapo—Chipangano Chatsopano?”

Iye anati, “Ine ndateropo.”

20 Ine ndinati, “Kodi inu mukuganiza chiani za Uthenga umene ine ndangowupereka kumene, wokhudza Iye kukhala yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse?”

Iye anati, “Ine ndikukhulupirira zimenezo.”

21 Ndipo ine ndinati, “Ndiye ngati Ambuye Yesu akanakhala ali moyo lero, Iye anakuchiritsani inu kale. Kunena za kuzunzika Kwake, izo nzotetezeka kale. Koma inu muyenera kukhala ndi chikhulupiriro. Ndipo ngati Iye akanakhala pano, Iye akanadziwa yemwe inu munali. Iye akanadziwa zomwe inu mwachita. Iye akanadziwa zonse za inu. Inu mukukhulupirira zimenezo?”

Iye anati, “Inde, bwana.”

22 Ine ndinati, “Ngati Iye ati awulule zimenezo, kodi inu mumukhulupirira Iye, ndiye, Iye adzakhala Mwana wa Mulungu, ndipo anawukitsidwa kwa akufa, ndipo ndi wamoyo kuno tsopano? Mzimu Wake mwa ine, ndi Akhristu ena awa?”

Iye anati, “Ine ndikukhulupirira zimenezo.”

23 Ine ndinati, “Chimene inu mwadzera pano. . . Amuna anu ndi aafupi, bambo wojintcha. Iye amasunga masharubu akuda. Masabata awiri apitawo, inu munali kwa dokotala. Dzina lanu ndi ili.” Ine sindinathe kulilemba, sindinathe kulinena ilo. Ine ndimayenera kulitchula ilo. Ilo linali dzina la Chimuhamedi.

Iye anati, “Zimenezo ndi zooni.”

24 Ndipo ine ndinati, “Ndiye, ndipo mwamuna wanu amadikirira mu holo. Iye anali atavala suti yotuwa komanso

chipewa chotuwa.” Ine ndinati, “Dokotalayo anali ngati munthu wamtali, woonda, wovala magalasi a khungwa la nyanga. Iye anakupimani inu mwachikazi, ndipo anapeza kuti inu munali ndi chotupa pa thumbo.”

Iye anati, “Izo ndi zoona.”

Ine ndinati, “Inu mukumuvomereza Yesu ngati Mpulumutsi wanu?”

Iye anati, “Yesu Khristu akhale Mpulumutsi wanga.”

Chotsatira chinali mnyamata wamng’ono wa maso otembenuzika.

²⁵ Ndipo iwo amangowalola amishonare kuti azipita, amatenga mmodzi kapena awiri kuchokera ku fuko lililonse. Iwe sukanakhoza kuwagwira iwo, panalibe njira nkomwe. Kotero, iwo anali ndi mahandiredi ndi mahandiredi a ankhondo akuyesetsa kuti awagwire iwo, ndipo iwo sakanakhoza kuchita zimenezo.

²⁶ Ndipo kotero ndiye mnyamata wamng’ono uyu, wa maso opingasa, iwo anamukhazika iye pa nsanja, pafupifupi mtunda wa *icho*.

²⁷ Ndipo pamwamba pa nsanja, akakombo aakulu a Calla awo. Alongo inu pano, amene mumakonda maluwa! Ena a maluwa a Calla amenewo ndi mainchesi eyitini kudutsa; achikasu, ojera, okongola. Ndipo anali nawo iwo. Iwo anangokhala akutchire. Anali ndi maluwa atakhala mozungulira.

²⁸ Ndipo ine ndinali kuyankhula. Iwo anadzamukhazika mnyamata wamng’onoyo pamwamba. Mmishonare anamukhazika iye pamwambapo. Ndipo mwana wamng’onoyo anali wa maso opingasa. Iye anali atangodya chakudya chake chamadzulo.

²⁹ Nthawizina zawo—zakudya zawo zimakhala zoseketsa kwambiri. Iye anali. . . Iwo amatenga kanthenga kakang’ono ndi kusomeka mtsempha wa ng’ombe, kulowa mu chimene iwo amachitcha chi—chidebe. Icho ndi kathumba kakang’ono, chikopa chosokedwa pamodzi, ndi kumasiya—magazi, magari otenthawo, azigwera mmenemo. Kenako nkukamira mkaka pang’ono mmenemo, ndi kuzisakaniza izo, izo zimapanga—suwiti ya mtengo yokoma.

Inu simungafune imodzi ya izo, sichoncho inu, wokondedwa? Ayi.

³⁰ Chotero zimenezo, koma, iye, ndizo zimene iye anakhala akudya. Ndipo maso ake aang’ono anapingasa. Ine ndinati, “Tsopano, aliyense akukhoza kuwona, angadziwe chomwe chiri cholakwika ndi mwanayu. Maso ake ndi opingasa. Ngati ndingakhoze kumuthandiza mwana ameneyo,” Ine ndinati, “Ndithudi ine ndikanachita zimenezo. Koma ine—ine sindingakhoze kuthandizira izo, chimodzimidzins

wina aliyenseyo.” Ine ndinati, “Ngati dokotala angathe, bwanji, ngati iye sangakhoze kuchita zimenezo, ndiye iye angakhale chinachake chimene dokotalayo angaipidwe nacho mu mtima, ngati iye angakhoze kuthandiza izo.” Ine ndinati, “Sindikuganiza kuti iwo angakhale ndi njira iliyonse yochitira pa nthawi ino.”

³¹ Ine ndinati, “Koma, tsopano, Ambuye akhoza kuwulula kwa ine za mwanayo.” Ndipo kenako, Iwo unati, “Mwanayo, bambo ake ndi amayi ake ndi awiri owonda.” Izo zinali. . . Iye anali wachi Zulu, ndipo iwo kawirikawiri amakhala onepa. Ine ndinati, “Awa ndi amenewo akhala pomwe apa tsopano. Dzina lawo ndi *lakuti-ndi-lakuti*.” Ndipo ine ndinati, ndiye, “Mwanayo anabadwa ndi maso opingasa. Chifukwa, amayi. . . Iwo amachokera ku a. . . Iwo amakhulupirira Chikhristu, chifukwa mkati mwa kanyumba kakang’ono, kaudzuko, muli chithunzi cha Khristu, chinapachikidwa ku dzanja lamanja la khoma.”

³² Ndipo ine ndinati, “Ndipo mwanayo, mwamsanga pamene mayiyo anamuwonetsa mwanayo kwa abambo ake, iye anali wa maso-wopingasa.” Abambo ndi amayi anaimirira, kuti atsimikizire kuti izo zinali zooni. Ine ndinayang’ana mmbuyo pa kamwanako, maso ake owongoka ngati anga.

³³ Chotero ndinati, “Tsopano, inu mukuona, Ambuye,” ine ndinati, “Ine sindinakhale mmapazi teni a mwanayo, mwanayo wachiritsidwa.”

Ine ndinangomudutsitsa iye. Ndipo ndinamuitana wotsatirayo.

³⁴ Ndiyeno pamene iye anatero, ine ndinamva phokoso. Dr. Bosworth ndi Dr. Ern Baxter, mamananjala anga, mu msonkhano, iwo anali akukangana ndi winawake, ndipo ine. . . kupangitsa chiphokoso choterocho. Munthu uyu anali akuyesetsa kuti apite pa nsanja, kapena akuyesetsa kuti apite pamwamba apo. Ndipo pamenepo panali madokotala angapo, madokotala azamankhwala atakhala pamenepo. Kotero dokotala uyu, iye—iye anati, iye anali kuyankhula. Iye anati, “Ine ndikufuna kuyankhula ndi iye za mwana ameneyo.”

Ine ndinapotoloka, ndinati, “Chavuta ndi chiyani, adokotala?”

Anati, “Inu munadziwa bwanji kuti ndine dokotala?”

³⁵ Ndipo ine ndinati, “Ndinu dokotala. Ndinu. . . Inu munakulira, ku England. Ndinu dokotala wachi British.” Ndipo ndinamuuzza iye kumene iye anachita sukulu.

³⁶ Iye anati, “Tsopano, Bambo Branham, ine ndikukhoza kumvetsa pamene kuwerenga maganizo kungakhoze—kungakhoze kuwerenga malingaliro anga.”

Ine ndinati, “Ine sindikuwerenga maganizo anu, adokotala.”

37 Ndipo iye anati, “Koma chimene ine sindingakhoze kumvetsa. . .” Anati, “Ine ndimakhulupirira kuti alipo Mulungu. Ndipo ine ndikudziwa kuti kakomboyo sangakhale pamenepo popanda Mulungu,” anati, “chifukwa iye ali ndi moyo mwa iye.” Iye anati, “Koma kodi Iye ndi wogwirika? Ine ndinamukhazika mwana ameneyo pa nsanja. Ine ndinamuyeza iye. Maso ake anali opingasa apo pomwe. Ndipo ndi uyu mwanayu tsopano ndi maso owongoka. Nchiyani chachita zimenezo, Bambo Branham?”

Ine ndinati, “Yesu Khristu.”

38 Ndipo iye anati, iye anati, “Chabwino, tsopano taonani,” iye anati, “Ine ndimakhulupirira mwa Mulungu.” Iye anati, “Koma ine ndikufuna kuti ndikufunensi inu funso, monga mtumiki tsopano. Kodi inu munamupepetula mwana ameneyo?”

39 Ine ndinati, “Bambo, ndipo inu mukutanthauza—Bungwe la British Medical Association limakupatsani inu chilolezo choti muchite zamankhwala, ndipo osadziwa zambiri za kupepetula kuposa zimenezo? Ngati kupepetula kungawongole maso a ana, inu muyenera kukhala mukuchita kupepetula.” Mukuona?

Ndipo iye anati, “Chabwino, ndiuzeni ine chimene chachita zimenezo.”

Ine ndinati, “Yesu Khristu.”

Iye anati, “Taonani,” anati, “Ine ndikukhulupirira. Ine ndinati Mulungu amakhala mu kakombo ameneyo.”

40 Ndipo Bambo Bosworth anati, “Tsopano, inu muyambitsa chipolowe pano.” Chifukwa, iwo anali ndi tsankho, nawonso, kumeneko, inu mukudziwa.

41 Ndipo kotero ine ndinati, “Inu mukuti. . .” Ndiye, nkhondo ya fuko. Ine ndinati, “Inu muyambitsa chipolowe tsopano. Musachite zimenezo.” Ine ndinati, “Inu mukutenga nthawi yochulukira kwambiri ya mwana ameneyo.”

42 Ndipo ine ndinati, “Apa pali chimene inu muyenera kuchita. Mwanayo anali ataimirira pamenepo. Inu mumuyike iye pa nsanja. Chikhulupiriro chake chomwe, ndi chikhulupiriro cha mayiyo, pomuwuza iye zimenezo, chamuchiritsa mwanayo. Maso ake anapingatsidwa pamenepo, iye sanandikhudze konse ine, kapena kukhala pondizungulira ine, kapena china chirichonse. Ine ndisanamuyang’ane nkomwe ndi kumuwona mwanayo, ndinayang’ana mmbuyo kwa osonkhana, ndinawona masomphenya, ndinanena chimene iwo anali, ndipo ndinayang’ana mmbuyo, maso a mwanayo anali atawongoka.”

43 Ndipo iye anadzayenda pansu pa choyankhulira chachikulu icho. Iye anati, “Ine ndikumuvomereza Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wanga.” Mukuona?

44 Pamene ine ndinali kuchoka ku Durban, iye analumphira pa mpanda, kumene ambiri, pafupifupi teni, anthu twente

sauzande anali kunja uko kuti asanzike, ndipo...Kapena, ndikuchoka (osati Durban, ine ndikupepesa) Johannesburg. Ndipo iye analumphira panja, ndipo anadzandigwira ine mchiuno, monga *chonchi*, ndipo anandiuza ine kuti iye anali atasiya ntchito yake mu mzinda, ndipo akutembenukira ku ntchito ya umishonare, ngati mmishonare wa zamankhwala kwa anthu. Ndipo pamene iye anali kuyankhula ndi ine, iye anayamba kuyankhula mmalirime ena, pamene iye anali kuyankhula ndi ine. Izo nzoona, dokotala wamankhwala, Anglikani, Anglikani.

⁴⁵ Wotsatira kumusi uko kunali mnyamata wamng'ono, kapena mnyamata wamng'ono. Iye...Ine sindikhala nayo nthawi yoti ndipite mu zimenezo. Ndizo...Iye anali chomwecho, iye—iye ankayenera kuti aziyenda ndi manja ake ndi mapazi, chomwecho. Iwo anali ndi unyolo atawuzinga pakhosi pake, ngati galu.

⁴⁶ Ndipo ine ndinati, “Mai, inu...” Munthu wosauka uyo, ngati aliyense angakhoze kumuthandiza iye, ndipo nkusiya kumachita zimenezo, iye angakhale munthu wamtima wankhanza kwambiri. Ine ndinati, “Ndithudi, tsopano, ine sindingathe kumuchiza iye, aliyense akudziwa zimenezo. Ine sindingakhoze kumuchiritsa iye. Ine ndikhoza kungonena ngati Ambuye ati andisonyeze ine zomwe zinachitika, kapena chimene chinayambitsa zimenezo, kapena chinachake. Chifukwa machiritso anagulidwa kale.”

⁴⁷ Tsopano, ine ndikufuna anthu inu pano, amene mukudwala, kuti muzindikire zimenezo. Machiritso anagulidwa kale. Inu munachiritsidwa kale. Ndi kusowa chabe kwa chikhulupiro. Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira. Inu muyenera kungokhulupirira izo tsopano.

⁴⁸ Ndipo kotero ndiye ife tikupeza kuti wamng'ono uyu... munthu uyu apa, ine—ine ndinati, “Mubweretseni iye kuno.”

⁴⁹ Ndipo iwo anali akumutsogolera iye pogwiritsa ntchito unyolo. Ndipo iye anaganiza, tsopano, nthawizina mitundu imafuna kuwachitira zitsuzo alendo. Ndipo iwo amavina pang'ono, inu mukudziwa, kavunidwe kakang'ono ka fuko, kuti atenge makobidi kuchokera kwa alendo odzacheza. Ndipo iye ankaganiza ine ndimafuna kuti iye avine. Mnyamatayo sanali bwino ngakhale mmaganizo. Ndipo, eya, ine sindikanakhoza kunena izi mu gulu losakanikirana ili, chifukwa iwo sankavala zovala, inu mukudziwa. Akazi awo, amuna, ndipo onse, ali maliseche. Kotero iwo—iwo basi...mwinamwake chilundu, kapena chinachake. Koma iye anali pa manja ndi mapazi ake, ndipo izo zinali zoipa basi. Kotero ndiye ine...Iwo anamugwira iye ndi unyolo, monga *choncho*, ndipo anamubweretsa iye pamwambapo; anali nawo pakhosi pake, akumutsogolera iye. Ndipo iye anali kuyesetsa, kumati, “A-ba-ba-ba.” Ine

ndinayesetsa kumupangitsa iye kuti amvetse kuti izo si zomwe ine ndimafuna. Ine. . .

⁵⁰ “Wotanthauzira Chizulu,” ine ndinati, “tsopano nenani mawuwo. Muwuzeni iye kuti ayime njii ndi kungokhulupirira.”

⁵¹ Ndipo iye anayang’ana mmwamba pa ine monga *choncho*. Ndipo—ndipo ine ndinati, “Tsopano, mnyamatayo ndi. . .Iye wakhala ali mwanjira imeneyo kuyambira ali kamunthu kakang’ono kwambiri.” Ine ndinati, “Chimene iye ali kwenikweni. . .Chimene iye akuchiganizira tsopano, ndi mchimwene wake. Mchimwene wake mwina anali atakwera pa galu wachikasu, kapena mbuzi. Iye anaponyedwa.” Ndipo ine ndinati, “Iye anadzilumalitsa yekha. Iye amayendera ndodo ziwiri.” Ndipo ine ndinati, “Tsopano, ine ndikuwona mnyamatayo wachiritsidwa. Iye, iye wataya ndodo zakezo.”

⁵² Pa nthawi imeneyo, zinatengera maminiti twente kuti iwo akhale chete. Mnyamatayo anali atakhala pafupifupi midadada itatu ya mzinda kunja uko, kumusi mwanjira *imeneyo*. Apa iye akubwera, ali ndi ndodo mmwamba mmanja mwake, akungothamanga mwamphamvu momwe iye akanamapitira. Iye anachiritsidwa, kumusi *uko*, pamene wotanthauzira wa Chizulu uja. Otanthauzira fifitini osiyanasiyana atayima pamenepo. Iwe ukanene mawu, umayenera kudikirira mpaka iwo atapita kudutsa mwa otanthauzirawo. Apa iye akubwera, ali ndi ndodo pamutu pake, monga *choncho*. Iye anachiritsidwa.

⁵³ Ndipo—ndipo kenako ine—ine ndinayang’ana pozungulira. Ndiye ine ndinazindikira, kachiwiri, ndikuyang’ana pa iye, ine ndinamuwona iye ataimirira. Ndiwo masomphenyawo. Palibe chimene chingaletse zimenezo. Ayi. Izo zatsirizidwa kale pamenepo, mwawona; ndikungoyembekezera mawu.

⁵⁴ Tsopano, penyani. Lolemba likubwerali ine ndikhala ndi zaka fifite-faivi zakubadwa. Ndi tsiku langa lobadwa. Ndipo ine ndakhala ndikuwona masomphenya kuyambira ndiri mnyamata wamng’ono. Ine sindinayambe ndawawona amodzi a iwo akulephera. Ndipo ine ndimufunsa aliyense ngati iwo anayamba awonapo amodzi, amene anayamba anenedwapo, anayamba alepherapo. Iwo sangakhoze kulephera. Ndi Mulungu.

⁵⁵ Kotero, ndiye ine ndinaziwona izo. Ndiye ine ndinaganiza, “Apa pali mwayi wanga tsopano kuti nditenge. . .kuti—kuti nditenge kuyitanira kuguwa kwanga. Ndipo ine ndinamuwona iye atayimirira. Ine ndinadziwa kuti iye akanachiritsidwa pamenepo, chifukwa, mwaona, izo zinawonetsedwa kale. Izo ziyenera kukhala mwanjira imeneyo. Ndi zomwe masomphenyawo ananena. Ndizo ndendende zomwe ziri zolondola.

⁵⁶ Ndi angati akudziwa kuti zinthu zimenezo ndi zoona? Izi, kuti alendo awone. [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Izo

nzoona. Ayi, palibe kulephera kwa izo. Mulungu nthawizonse amazipanga izo kulondola.

⁵⁷ Ine ndinaganiza, “Iyi ndi nthawi yanga yoyitanira kuguwa.” Ine ndinati, “Tsopano, mnyamata uyu apa, ine sindingakhoze kumuchiritsa iye. Koma ngati mphamvu ya Mulungu yandiwonetsa ine masomphenya, ndiye iye achiritsidwa tsopano. Tsopano, ngati iye sachiritsidwa, ndiye ine ndine mneneri wabodza. Koma ngati iye achiritsidwe, ndi angati a inu kunja uko muti mumulandire Khristu ngati Mpulumutsi wanu?” Uko kunali, ine ndikuganiza, uko kunali Achimuhamedi teni sauzande kumeneko.

⁵⁸ Ine ndinangoyankhula, masiku pang’ono izo zisanachitike, kwa munthu waluntha. Anati, “Chikho chodalitsika chimenecho!” Inu mukudziwa, iwo anachokera kwa Amedi-o-Persia akale. Iwo samasintha kapena kusintha. Inu simungakhoze kumusintha mmodzi wa anyamata amenewo.

⁵⁹ Kotero, ndipo apo iwo anali, atakhala pamenepo. Mmodzi wa akazi Achimuhamedi anali atangomulandira kumene Khristu, ndipo izo zinawakopa iwo. Ndipo mwana wamwamuna wa Mahatma Gandhi anali komweko.

⁶⁰ Chotero, apo panali—apo panali mnyamata uyu. Ndipo kotero ine ndinati, “Imirira pa mapazi ako. Yesu Khristu wakuchiritsa iwe.” Chabwino, iye anayesera kuti azipita, “Ugu-ugu-ugu,” monga choncho. Ine ndinayenda ndi kukatenga unyolo m’manja mwanga. Ine ndinati, “Imirira. Yesu Khristu wakuchiritsa iwe.”

⁶¹ Tsopano, apa pali Baibulo. Ndipo ngati inu nonse mukudziwa ndiye zomwe zachitika mmausiku angapo apitawa, Ine sindingayerekeze kunena chirichonse chomwe chingakhale cholakwika, mu izi.

⁶² Kumeneko, mnyamata ameneyo anali kusautsika monga choncho, anayenda, nsana wake ukugwedezeza kulowa mkati, ngati kavalo wogwedezeza. Manja ndi mapazi ake; manja ake anali olimba basi monga mapazi ake, chifukwa cha kuyenda. Kwa nthawi yoyamba mmoyo wake, anaima pa mapazi ake. Misozi imagwera kuchokera pamimba pake pakuda, monga *choncho*, imangoyenderera pansu, chomwecho. Osati kokha iye anachiritsidwa, koma anayamba kumaganiza bwino bwino. Mukuona?

⁶³ Ine ndinawona, ine ndinati, “Tsopano kwa inu nonse amene muti mukhulupirire, mutakhulupirira tsopano pamene ine ndikupemphera. Ine ndikufuna kuti ndidziwe kuti ndi angati pano,” Ine ndinati, “amulandire Khristu ngati Mpulumutsi?” Ndipo panawoneka ngati nyanja. Ndipo iwo analembetsa mbadwa za mabulangete sarte sauzande, amene sankadziwa kusiyanita kwa dzanja lamanja ndi lamanzere, anabwera kwa Khristu.

64 Ine ndikukumbukira ndikuyankhula kwa a Kiwanis, osati kale litali. Ndiyeno ine ndikukumbukira munthu amene anandidzoza ine mu mpingo wa Mishonare Baptisti, yemwe nthawizonse ankandiseka. Ine ndinati “Zomwe Bap-... Chimene inu mumachitcha kutentheka, mwaona, chapindulira miyoyo yambiri kwa Khristu mu ora limodzi, kuposa teni sauzande a madola omwe mpingo wa Baptisti wayika mmamishonare kumeneko.

65 Kodi ife tinawapeza chiyani iwo? Cha kumeneko, ataikidwa ngati Mkhristu, monga *chonchi*, ndipo atanyamula fano mu nkono mwawo. “Ngati Amoyah...” *Amoyah* amatanthauza “mphamvu yosawoneka,” ngati mphepo. “Ngati iye angalephere, *uyu* sangalephere.” Ndiyo mphamvu ya izo. Ndipo pamenepo ine ndinawona mbadwa za mabulangete sarte sauzande zikupereka moyo wawo kwa Khristu.

66 Ndi kumapita ku mafuko kunjira uko, zikuwatengera abwenzi awo enawo kwa Khristu. Ndipo ine ndinapanga pemphero limodzi la gulu lonselo. Ndipo pafupifupi maora foro kuchokera pamenepo, Sidney Smith, meya wa Durban, Sidney Smith, meya wa Durban, South Africa, anandiyimbira ine foni. Chimene, panali mkazi yemwe anali atamwalira, usiku wadzana, ndipo ndinaitanidwa, kuti ndipemphere. Ndipo iye anali pa msonkhano, wamoyo. Ndipo koteri, ndiye, ameneyo anali wachibale wa Sidney Smith, ndipo iye anali yense atakondowezeke.

67 Ndiyeno pamene izi, iye anati, “Pita pa zenera lako ndipo ukawone, akutsika pansu mu msewu;” Ndipo apo pamabwera mavani aakulu amenewo, atangowunjikidwa modzaza. Ndipo mbadwa zomwe zinali mmabedi amenewo ndi machira, mmawa umenewo, zinali zikuyenda kumbuyo kwake, ndi manja awo mmwamba, zikulira, zikuimba mchinenero chawo, “Kungo khulupirira. Zinthu zonse ndi zotheka.” Ndipo panalibenso nkondo pakati pawo, mzere pambuyo pa mzere akubwera kumatsikira kumeneko. Magalimoto akupita monga choncho, ndipo apolisi operekeza, ndi njinga zamoto zinkayenera kumathamanga paliponse, monga choncho. *Kungo Khulupirira*.

68 Tsopano, ngati mbadwa zabulangete zomwe sizimadziwa kusiyantsa kwa kumanja ndi kumanzere zinakhoza kuvomereza zimenezo, nanga bwanji ife? Mukuona? Inu mukudziwa chifukwa chake? Iwo sanadzazidwepo ndi mtundu uliwonse wa chiphunzitsi. Mukuona?

69 Ife takhalapo ndi aliyense. Dr. *Akuti-ndi-akuti* akuti, “Ndi kutengeka.” Wina uyu akuti, “Ndi kuwerenga maganizo.” Uyu akuti, “Palibe kanthu kwa izo.” Uyu akuti, “Ndi mdierekezi.” Iwe sumadziwa choti ukhulupirire. Ndi chifukwa chake zimakhala zovuta. Malo ovuta kwambiri kuti ukhale ndi misonkhano ya machiritso ndi mu U.S.A. Uko nkulondola.

⁷⁰ Kumeneko, iwo kumeneko, iwo samadziwa kanthu za izo. Iwo sanamvepo kalikonse. Iwe ukawawuza iwo. Iwo amakhala ngati mwana. Iwo amavomereza izo ndi kuzikhulupirira izo, akatero amakhala akupita.

⁷¹ Ambuye atithandize ife tsopano. Tsopano, nthawi imodzi yokha kuti tipemphere. Ife sitingakhoze kupemphera kochuluka, ndicho chinthu chimodzi. Baibulo linati, “Ine ndikanafuna kuti amuna azipemphera paliponse, atakweza manja oyera mmwamba.”

⁷² Tilandireni ife, Ambuye, mu chiyanjano Chanu pano, pamene ife tikudzipereka tokha kwa Inu, chiyanjano cha Mawu Anu, pakuti Inu ndinu Mawu. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu, yakhulani kwa mitima. Amenii.

⁷³ Ife tinamusiya Abraham usiku watha mu. . . Ife tinayamba ndi iye, ndipo uko mu mutu wa 22 wa Genesis, kumene iye anali akumpereka mwana wake yekhayo, choimira cha Mulungu akumpereka Mwana Wake. Ife tinayambira kumbuyo kumeneko, tinabwereranso kuti tidzamutengenso iye kachiwiri, moyo wake, ndipo ife sitinachoke kwa izo panobe. Ife tinamusiya iye, usiku watha, cha pafupifupi mutu wa 16 kapena wa 17. Ine ndikukhulupirira, mutu wa 15 ndi pamene ife tinamusiya iye. Ndipo ife tiyesetsa kuti timalizitse zimenezo usikuuno, chifukwa ndiri ndi uthenga wa machiritso Auzimu basi, Ambuye akalola, wa mawa madzulo.

⁷⁴ Ndipo tsopano m’busa aliyense akuitanidwa. Mudzabweretse osonkhana anu. Mudzabwere kuno ndi kudzayima nawo iwo kwa pemphero.

⁷⁵ Tsopano ife tikuzindikira kuti nthawizina Yesu ankachita zinthu, ndipo Iye nthawizina amachita zinthu. . . Inu mukuti, “Ndi chifukwa chiyani ndiye kuti Iye amaloleza zinthu zimenezi, M’bale Branham? Ndi chifukwa chiyani Iye amaloleza zinthu zimenezi kuti zikhalepo?” Nthawizina izo zimachitika kuti ziyese chikhulupiriro chanu, nthawi zambiri. Ife. . . Ndipo Iye amachita zinthu mwachilendo. Bwanji Iye samangoyenda ndi kunena kuti, “Ine ndine *Ichi*, ndipo Ine ndine *Icho*.” Iye sanachite zimenezo kuyamba ndi kuyamba. Mwaona, Iye amachita zimenezo kuti ayese chikhulupiriro chanu.

⁷⁶ Taonani, ansembe ankaganiza kuti mwinamwake Iye akanabwera kudzayankhula kwa Kayafa, wansembe wamkulu. Koma kodi Iye anabadwa motani? Mu khola. Ndipo anakanidwa mwamtheradi ndi anthu Ake Omwe ndi zipembedzo Zake za masiku amenewo.

⁷⁷ Tsopano ife tikupeza, nthawi ina, Yesu akuyankhula. Ine ndikungofuna kuwona chobwereza chimodzi chaching’ono apa chimene ine ndikufuna kuti ndipange. Yesu ali ndi gulu lalikulu lomuzungulira Iye, ndipo izo zikuwoneka ngati pali ochuluka kwambiri, kotero penyani zimene Iye ananena. “Kupatulula inu

mutadya thupi la Mwana wa munthu, ndi kumwa Magazi Ake, inu mulibe Moyo.” Tsopano kodi inu mukuganiza kuti dokotala wazamankhwala, kapena munthu aliyense waluntha, akanaganiza chiyani pamene iwo anamva za Munthu yemwe anali ndi dzina la kukhala mwana wapathengo ndipo wochuluka ngati chigawenga kwa anthu a tsiku limenelo, kuimirira ndi kupanga cho—chobwereza monga chomwecho, “Pokhapokha inu mutadya thupi Langa ndi kumwa Magazi Anga”?

⁷⁸ Bwanji, iwo akanati, “Munthu ameneyo ndi mthakati wa munthu. Bwanji, mai! ‘Kumwa Magazi a Munthu, ndi kudya mnofu Wake’? Osonkhana inu chokani kwa Munthu wopenga woteroyo.”

⁷⁹ Iye sanazifotokeze konse zimenezo. Iye sanazifotokeze konse zimenezo. Iye sankasowa kuti afotokeze zimenezo. Uko nkulondola. Iye ankangofuna kuti awone kuti iwo anali ndi chikhulupiriro cha mtundu wanji.

⁸⁰ Mukuona, inu, ngati iwe ukukhulupirira, iwe ukukhulupirira, ine sindikusamala zimene aliyense akunena. Ngati nditapempherera anthu faivi sauzande usikuuno, ndipo faivi sauzande onsewo nkufa usikuuno, m'mawa ine ndingakhale ndikupempherera odwala. Mukuona? Ndi zomwe Mulungu amanena, ndi zomwe zimafunikira. Si zomwe anthu amachita. Mukuona?

⁸¹ Ndipo, Mulungu, Iye—Iye anati, “Ndipo pokhapokha inu mutadya mnofu wa Mwana wa munthu, ndi kumwa Magazi Ake, inu mulibe Moyo mwa inu.”

⁸² Chabwino, mai, anthu amenewo, gulu laluntha lija, bwanji, bwanji, iwo anati, “Chokani kwa Munthu ameneyo. Iye ndi wamisala. Iye ndi munthu wakuthengo. Bwanji, Iye ndi mthakati wa munthu, ‘kudya’ thupi la Munthu ameneyo.” Tsopano, Iye sanazifotokeze konse zimenezo.

⁸³ Tsopano Iye anali nawo alaliki odzodzedwa sevente limodzi ndi Iye. Iye ankaganiza kuti Iye anali ndi gulu laling’ono kwambiri kumeneko—gulu la anthu linamuchokera Iye. Kotero Iye anali ndi atumiki odzodzedwa atakhala pamenepo, amene Iye ankawatumiza kunjira, sevente a iwo. Iye anati, “Kodi inu mudzanena chiyani pamene inu mudzamuwone Mwana wa munthu akukwera Kumwamba kumene Iye anachokerako?” Tsopano, Iye sanazifotokeze konse zimenezo.

⁸⁴ Ndipo alaliki amenewo anati, “Munthu uyu kukwera Kumwamba kumene Iye anachokerako? Bwanji, ife tikumudziwa Iye. Ife tikuwadziwa amayi Ake. Ife takhalako ku khola kumene Iye anabadwira. Ife tinawona bedi imeme Iye anagonekedwamo. Ife timawedza ndi Iye. Ife tikumagona kunjira kuno pa magombe ndi Iye. Ndipo Mwana wa munthu uyu ‘kukwera kumene Iye anachokera’? Iye anachokera ku Betelehemu. Kodi izi, ‘zikupita kuti’? Izo ndi zotichulukira

kwambiri ife.” Ndipo iwo anachoka kwa Iye. Iye sanazifotokoze konse zimenezo. Iye sanatero.

⁸⁵ Iye sankasowa kuti afotokoze kalikonse. Mulungu samasowa kuti afotokoze kalikonse. Iye ndi Mulungu. Iye amangochita izo, chifukwa Iye analonjeza izo. Iye samazifotokoza izo.

⁸⁶ Ndiye thwelovu Ake okha anatsalira. Ndipo Iye anapotoloka ndipo anayang’ana pa iwo, anati, “Ine ndasankha thwelovu a inu, ndipo mmodzi wa inu ndi mdierekezi.” Iye anati, “Kodi inu mukufuna kupita, inunso?”

⁸⁷ Kenako Petro ananena mawu aakulu amenewo “Ndi kwa ndani ife tingapiteko, Ambuye? Pakuti ife tiri otsimikiza kuti Inu muli nawo Mawu a Moyo.” Iwo anali atawawona Iwo momveka bwino akutsimikiziridwa; ziribe kanthu zomwe ansembe ankanena, zomwe wina aliyense ananena. Iwo ankadziwa apo pomwe, kuti, Iye anali nawo Mawu a Moyo. Anati, “Inu muli nawo Mawu a Moyo.”

⁸⁸ Ndipo tsopano ife tikuzindikira, ziribe kanthu zomwe enawo anachita, momwe iwo anachokerapo, ophunzira amenewo anakozedweratu, iwo anadzodweratu ku Moyo Wamuyaya. Ayi, iwo sakanakhoza kufotokoza Izo, iwo sakanakhoza kufotokoza Izo mochuluka kuposa momwe iwo ena onse akanachitira. Koma munali chinachake mwa iwo, chimene—choyimira chija Kumwamba. Lingaliro limene Mulungu anali nalo la iwo asanaikidwe maziko a dziko lapansi, anali atadziwonetsera okha apa, ndipo iwo anali olumikizana ndi Mulungu ndipo anali otsimikiza kuti limenelo linali lonjezo la Mulungu lotsimikizidwa, ndipo palibe chimene chiti chisinthe izo kwa iwo. Ndicho chenicheni, Chikhristu chenicheni.

⁸⁹ Lero, anthu ali chinachake mwadongosolo monga iwo analiri mmasiku pamene ophunzira anali panyanja. Ndipo usiku wina kunadza namondwe, ndipo apo panalibe kanthu; ziyembekezo zonse zinali zitapita, kuti iwo adzapulumutsidwa konse. Ndipo anamuwona Iye akubwera, akuyenda pa—a—madzi. Tsopano ngalawa yawo inadzadza madzi, ndipo matanga anasweka, ndipo zopapasira zinali zitapita, ndipo iwo anali akugwirana wina ndi mzake, akukuwa. Ndipo iwo anayang’ana kunja uko ndipo anamuwona Iye akubwera, akuyenda pa madzi, ndipo anachita mantha ndi Iye. Chiyembekezo chawo chokhacho, ndipo iwo ankachita mantha ndi chinthu chokhacho chimene chikanawapulumutsa iwo. Ngati icho sichiri chithunzi chowona lero, kachiwiri! Iwo—iwo ankaganiza kuti izo zinkawoneka zipukupuku. Inu mukudziwa, iwo anati iwo analira, chifukwa cha mantha, “Ndi mzimu!” Izo zinkawoneka ngati zauzimu kwambiri. Ndicho chinthu chomwecho chimene chiripo lero.

⁹⁰ Koma ngati inu mutangochita monga iwo anachitira pamene iwo analira; iwo anamva liwu lija likubwera, “Musawope ayi. Ndi Ine. Musachite mantha. Khalani olimbika mtima.”

⁹¹ Ndipo ngati inu mutangoyang'ana Mawu a lonjezo a tsiku lino, inu mudzamva liwu lomwelo likuyankhula kudzera m'Mawu, "Ndi Ine. Ine ndinalonjeza kudzachita izi mmasiku otsiriza. Musawope ayi. Musachite mantha. Muike chidaliro chanu mwa Ine, Mwana wa Mulungu," Yemwe Iye ali. Khulupirirani izo tsopano.

⁹² Ife tinamusiya Abrahamu mu Kukhalapo kwa Elohim, usiku wathawu, kumene iye. . . Ife tinamubweretsa iye kudutsa mu malonjezo. Ndipo tsopano lonjezo lotsiriza kusanachitike kudza kwa mwana, ife tikupeza kuti Munthu anabwera pamenepo; atavala ngati munthu, akudya ngati munthu, akuyankhula ngati munthu; ndipo Abrahamu anayang'ana pa Iye ndipo anamutcha Iye Elohim, "Elohim." Awiri anali atapita ku Sodomu, kukalalikira kumusi kumeneko. Ndipo ife tinafanizira chochitika chimenecho ndi lero. Inu nonse mukuikumbukira nkhaniyo pamene ife tinayisiyira iyo. Mwangwiro basi chinthu chomwecho monga Yesu ananeneratu kuti icho chikanadzakhala, kuti, "monga zinali mmasiku a Sodomu," chinthu chomwecho chikukhala mmalo omwewo usikuuno. Ndipo ngati. . .

⁹³ Lero ine ndinali nditakhala pamenepo, ndipo ine ndinali kudabwa, ndipo ine ndinadabwa zonse za izi. Iwo anamva chivomezi china chikuchitika kumusi uko, ndipo iwo anati, "Kugwedeza mayiko kachiwiri." Ndipo ine ndinaganiza, ichi ndi chiyani? Inu mukudziwa, izo zinachitika Lachisanu Labwino. Inu mukudziwa, zaka naintini handiredi zapitazo, pa Lachisanu Labwino, mpingo unamukana Yesu Khristu, ndipo chivomezi chinagwedeza dziko lapansi lonse. Ndipo iwo amukana Iye kachiwiri, mu M'badwo wa Laodikaya, monga Baibulo linati iwo akanadzachita, anali naye Iye kunjja.

⁹⁴ Ndipo kusuntha kwa zipembedzo uku kwa Bungwe la Mipingo ndi ndendende zimene iwo akuchita. Iwo akutaya ziphunzitsa zawo zonse za uvangeli ndi zinthu. "Awiri angayende bwanji limodzi pokhapokha iwo atagwirizana?" Chabwino, inu simungakhoze kuchita zimenezo.

⁹⁵ Izo sizingagwire ntchito ndi Akhristu enieni, enieni. Iwo sadzachelandira konse icho. Ayi, bwana. Mkhristu wobadwa mwatsopano sadzapita konse mu msampha wonga umenewo. Izo ziri ngati kuika bakha mu—mu khola. Iwo amadziwa kuti iye walunjika kokaphedwa. Inu simudzamufikitsa konse iye mu zimenezo. Kotero ife. . . Mkhristu weniweni wobadwa mwatsopano adzakhala kutali ndi zimenezo.

⁹⁶ Tsopano Abraham anali atayima pamenepo ndi kumayankhula ndi Mwamuna yemwe anali atatembenuzira nsana Wake ku hema kumene Sarah anali. Ndipo Abram. . . Dzina la Abraham, tsiku limodzi kapena awiri izo zisanachitike, linali Abram; ndi Sarai, ndipo tsopano ndi Sarah, kwa

Abraham. Ndipo Iye anamutcha Abraham mu dzina lake lautate, launsembe. “Abraham, ali kuti Sarah (*kalonga*) mkazi wako?”

Iye anati, “Iye ali mu hema, kumbuyo Kwanu.”

⁹⁷ Iye anati, “Ine ndidzakuchezerani inu molingana ndi lonjezo, nthawi ya moyo,” mwakuyankhula kwina, “mwezi wina. Ndipo ine ndidzakuchezerani inu monga Ine ndalonjezera.”

⁹⁸ Anakhala akudikirira kwa zaka twente-faivi tsopano pa mwana wolonjezedwa uyu; osazandima kwa kusakhulupirira pa Mawu a Mulungu, koma anali amphamvu, akupereka matamando kwa Mulungu. Penyani izi tsopano.

⁹⁹ Ndiyeno Sarah, mkati mwa hema, ngati tingaziyike izo mu kanenedwe ka mu msewu, anakhala ngati anasekera pa nkono wake, anati, “Ine, mkazi wachikulire, wa zaka nainte zakubadwa, ndipo kukhala—kukhala ndi chisangalalo ndi mbuye wanga, mwamuna wanga, iye kunja uko zaka handiredi zakubadwa?” Anasiya kukhala ngati mwamuna ndi mkazi; zaka zambiri, zambiri.

¹⁰⁰ Ndipo—ndipo Munthuyo, atatembenezira nsana Wake ku chihema, anati, “Ndi chifukwa chiyani Sarah anakayikira zimenezo, ponena mu mtima mwake zinthu zimenezi?” Mukuona? Ndipo mwanjira imeneyo Abrahamu anazindikira Yemwe anali kuyankhula ndi iye. Uyo anali Elohim, ndendende. Chizindikiro Chake chinatsimikizira chodzinerera Chake. Anati, “Ine ndidzakuchezerani inu.” Chifukwa chiyani Iye anati, “Ine”? Kodi Iye anamutcha bwanji iye Abrahamu? Pamene, Iye anali Mmodzi yemwe anamupatsa iye dzinalo. Mu chophiphiritsa, osati mu kukhalapo kwa munthu; kusonyeza ndendende zomwe zikanati zidzachitike. Mpatseni iye ulamuliro Wake wotsimikiziridwa ndi Mawu olonjezedwa, kuti Munthu uyu yemwe anali kuyankhula kwa iye anali Mulungu, Elohim.

¹⁰¹ Tsopano ife tikupeza, mu Ahebri mutu wa 4 ndi ndime ya 12, monga ine ndabwereza izo kawiri, kale, mausiku angapo apitawa, kuti, Baibulo linati, “Mawu a Mulungu amazindikira malingaliro amene ali mu mtima, zinsinsi za mu mtima.”

¹⁰² Ndipo pamene Yesu anakhoza kuyang’ana pa osonkhana ndi kuzindikira malingaliro awo, ndipo anamuza mkaziyo amuna amene iye anakhala nawo, ndipo anamuza Natanaeli kumene iye anali, uko kunali kutsimikizira kuti Iye anali Mesiya uja, Mulungu, Emanuele, chifukwa Iye anali Mawu.

¹⁰³ Umo ndi momwe aneneri ankakhalira. Aneneri ankatengedwa ngati amulungu. Inu mukumvetisa zimenezo. Yesu ananena chomwecho, Iyemwini. Anati, “Inu mungakhoze bwanji kunditsutsa Ine? Pamene, inu mukuwatchesa iwo amene Mawu a Mulungu amadza kwa iwo, inu mumawatchesa iwo ‘amulungu’. Ndipo momwe inu mukunditsutsira Ine, pamene Ine ndikuti, ‘Ine ndine Mwana wa Mulungu’? Ndipo ngati Ine

sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musakhulupirire zimenezo.”

¹⁰⁴ Iye anali Mawu otsimikiziridwa a Mulungu a m’badwo umenewo. Tsopano ngati Iye akanabwera ndi chizindikiro cha Mose, icho sichikanakhoza kugwira ntchito. Ngati Mose akanabwera ndi chizindikiro cha Nowa, icho sichinaloseredwe izo kwa tsiku limenelo.

¹⁰⁵ Ndipo azibusa onse awa, ndi zafioloje, ndi masukulu apamwamba, ndi masukulu, ndi atumiki ophunzira; zomwe ziri zabwino, ife sitikutsutsana nazo izo, koma umenewo si Uthenga wa orali. Izo zinali za tsiku lolunda lija.

¹⁰⁶ “Kudzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo.” Iye analonjeza zinthu izi. Ine ndaziwerenga izo mobwereza bwereza, kuchokera mu Mawu. Ndendende monga izo zinali nthawiyo, Iye anati izo zidzakhala kachiwiri. Ine ndikhoza kumangiriza izo ndi Lemba lirilonse mu Baibulo, ndi kukusonyezani inu kuti izo ndi Choonadi.

¹⁰⁷ Tsopano, zozinenera Zake pamenepo zinatsimikiziridwa pamene Iye ananena yemwe, Sarah, zimene iye anachita kumbuyo kwa Iye. Tsopano zindikirani, Iye analonjeza, mwezi wamawa iye adzakhala ndi pakati, “malingana ndi nthawi ya moyo,” Iye anatero.

¹⁰⁸ Tsopano zindikirani, njira ya Abrahamu inali choyimira cha Mbewu yachifumu tsopano. Ngati inu mungazindikire, Abraham, lonjezo linali kwa iye ndi kwa ana ake a pambuyo pake. Ndiyeno ana ake anali, choyamba, mbewu yachibadwa, ndipo kenako Mbewu yachifumu yomwe inali Khristu. Mbewu yoyamba, yomwe inali mwa kugonana, kunadza Isaki; koma popanda kugonana, kunadzabwera Yesu, Mbewu Yachifumu.

¹⁰⁹ Tsopano zimenezo, Magazi, mwaona, ife timapulumsidwa mwa Magazi. “Ndipo popanda kukhetsedwa kwa magazi, palibe chikhululukiro.”

¹¹⁰ Zindikirani, Yesu sanali Myuda. Yesu sanali Wamitundu. Yesu anali Mulungu. Iye sanali, Iye sakanakhoza kukhala Myuda kapena Wamitundu. Taonani, chachimuna chimatulutsa moyo wamagazi, womwe uli khungu la magazi. Nyongolosi imakhala mu khungu la magazi.

¹¹¹ Ine ndikumakumvani anthu inu pano, ambiri a inu. . . Ine ndinali kuyenda mozungulira tsiku lina, ndikuyang’ana anu—alimi anu, ndipo inu muli ndi nkhuku. Tsopano, nkhuku ikhoza kuyikira dzira, mayi wachikulire mbalame akhoza kuyikira dzira; koma ngati iye sanakhale ndi mwamuna ameneyo, iye sadzaswa konse. Komabe, iye akhoza kuikira dzira, pakuti dzira limakhala mu—mu. . . mwa mkazi. Koma, magazi, ndi moyo zimakhala m’magazi.

¹¹² Chotero, chomwecho, moyo Wake unali moyo wolengedwa, wosapatsidwa moyo kuchokera kwa mwamuna wina.

¹¹³ Ndiyeno dziralalo silinali Mariya, chifukwa ngati dziralalo linali Mariya...Monga momwe Achiprotetanti ambiri amakhulupirira, ndi Akatolika, nawonso, kuti dzira linali Maria, tsopano ndi...linali dzira la Mariya, kumupanga Iye munthu. Ayi, ngati khungu la magazi linali Mulungu, chomwechonso dzira linali la Mulungu, chifukwa Mariya sakanakhoza kulibweretsa dzira limenelo pansi...Inu mukudziwa, inu mukumvetsa zomwe ine ndikuzikamba. Iye...Iye sakanakhoza kuchita zimenezo popanda zogirigisha. Chotero, ndi—ndi mugirigisha, kodi inu mukumupangitsa Mulungu kuchita chiyani ndiye? Kukhala kugonana kachiwiri. Mukuona?

¹¹⁴ Chotero ziwiri zonse dzira ndi khungu la magazi zinali Mulungu. Amen. Ndizo...Mukhulupirire zimenezo, ndipo inu mudzakhala ndi chikhulupiriro choyenda kumapita mtsogolo. Ife sitinapulumsidwe ndi magazi Achiyuda, kapena ndi magazi a Amitundu. Ife timapulumsidwa ndi Magazi a Mulungu, Iyemwini, khungu la Magazi lolengedwa.

¹¹⁵ Monga ine ndinanena, mutenge mbalame za kholo zakale izi. Ikubwera nthawi yamasika. Ine ndinali kuzindikira tsiku lina, momwe izo zimatengera udzu ndi kupita mmwamba ndi kukapanga zisa zawo. Tsopano iyo ikhoza kufika pamwamba apo ndi kukapanga chisa, ndi kukaika chisa chodzaza ndi mazira; ndi kukakhalira pa iwo, ndi kuwafungatira iwo, ndi kukhala wokhulupirika kwambiri kwa mazira amenewo mpaka iye—iye amakhoza kusauka kwambiri osatha kuwuluka kuchoka pa chisacho, kuti akazipezere chinachake choti adye. Koma ngati iye sanakumane ndi mbalame yaimuna, iwo sadzaswa konse. Iwo samakhala achonde. Inu mukudziwa zimenezo. Iwo adzakhala mu chisacho, ndi kuvunda.

¹¹⁶ Ndipo umo ndi momwe ina ya mipingo yathu imachitira. Ife tangokhala ndi chisa chodzadza ndi mazira ovunda. Iwo alibe chikhulupiriro cha Abrahamu. Ndi nthawi yokonza chisa ndikuyamba kubwerera, kukhudzana; osati ndi bungwe lina, seminare ina ya zafioloje. Koma kulumikizana ndi mwamunayo, Khristu Yesu, Yemwe amabweretsa chonde ku Mzimu wa Moyo umene uli mwa inu. Iye ndi Mmodzi yemwe amakupangitsani inu kukhulupirira Izo. Konzani chisacho ndipo muyambirensa kachiwiri. Inu mumawasisita iwo pa nsana ndi kuwatengera iwo mkati, ndi kuwapanga iwo madikoni, ndipo anakwatirapo kaforo kapena kafaivi, ndi chirichonse. Dziko liti lomwe ife tikubwerako, mulimonse? Atumizeni iwo ku seminare ndi kubayamo ena a mankhwala owumitsira mitembowo, ndi kuwabweretsanso iwo.

¹¹⁷ Ndipo kuno tsiku lina, pakuyerekeza, zinasonyeza kuti nainte-naini pa handiredi a alaliki Achiprotetanti mu fuko

lonselo, samakhulupirira za Kudza Kwachiwiri kwenikweni kwa Khristu. Eyite-seveni pa handiredi amakana kubadwa kwa namwali. Taganizani za zimenezo. Nchiyani ana athu ati akakumane nacho kutaliko?

118 Mulungu, tibwezeretseni ife ku Chikhulupiriro kachiwiri chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera.

119 Abrahamu, penyani njira yake pamene iye akubwera, iye anaimiridwa ndendende ndi mpingo. Zonse zimene Abrahamu anachita, ziri...Ife tawupenya mpingo. Ngati ife tikanakhala ndi sabata kapena awiri pano, kuti tikhale pano, ine ndikanakhoza kukusonyezani inu, sitepe ndi sitepe. Mpingo wapanga njira yomweyo. Chizindikiro chotsiriza chinali Mulungu, Mawu olonjezedwa akuyankhula kwa iye, mu thupi laumunthu. Lonjezo lotsiriza dziko la Amitundu lisanawonongedwe, lomwe linali Sodomu ndi Gomora. Tsopano taganizani, Abraham, kale, analipo...Mulungu anali atawonekera kwa iye mu zizindikiro zambiri, ndi kuwala, ndi mawonekedwe, ndi zizindikiro, koma Mulungu anali asanabwere kwa iye monga munthu ndi kuyankhula ndi liwu lomveka, monga munthu wokhalapo, kuchokera mwa munthu wokhalapo. Ndipo, kumbukirani, lonjezo tsopano lakonzekera kuti likwaniritsidwe, Sodomu awotchedwa, uthenga wotsiriza uli mkati.

120 Ndipo apo pakupita mpingo mwachizolowezi, chipembedzo cha mpingo, kani. Uko, uko kukupita Billy Graham wamakono kumusi uko, kuti awatulutse iwo.

121 Uko kuli Mpingo Wosankhidwa, osati mu Sodomu; woitanidwa utuluke, kulekanitsidwa. Iwo amupeza mtumiki. Zindikirani, gulu la Abrahamu linalandira Uthenga. Ndipo tsopano chinali chiyani chimenecho? Mulungu, yemwe anakhala akuyankhula ndi iye nthawi yonseyo, mu zophiphiritsa ndi mawonekedwe, ndi chirichonse, anabwera apo pomwe. Ndipo tsopano Iye akudziwonetsera Yekha pomwe pano mu thupi la munthu, ndipo akuzindikira lingaliro lomwe linali mu mtima wa Sarah, kumbuyo kwa Iye. Ndipo Abraham anati, “Ndi Elohim, Mmodzi Wokwanira mu Zonseyo.” Kumbukirani, mwamsanga zitachitika zimenezo, Sodomu anawotchedwa. Taganizani za zimenezo.

122 Mpingo ukhoza kukhala ukulandira chizindikiro chake chotsiriza. Mwaona, tatero...Inu mwafuula, inu munalungamitsidwa ndi Luther; kuyeretsewa ndi Wesley, nthawi yopambana, kufuula, kusangalala; kuyankhula mmalirime, kutanthauzira kwa malirime, machiritso Auzimu. Koma ife tiri kuti tsopano? Mulungu akuyankhula pakati pathu pomwe, kupyolera mwa ife, momveka, chimodzimodzi monga momwe Iye anachitira pamenepo. Ndipo Iye analonjeza kuti adzachita zimenezo. Ndicho chinthucho. Si chinachake chimene

ife tinapanga. Baibulo linanena chomwecho. Yesu anati Iye akanadzachita izo, kudzipanga Yekha kachiwiri.

¹²³ Zindikirani, ndipo mwamsanga zitachitika izi, Abraham anachonderera mmalo mwa Loti. Ndipo Iye anati ngati Iye angakhoze kukapeza ngakhale anthu teni, Iye akanati awapulumentse iwo. Koma Iye sanakhoze ngakhale kuwapeza amenewo, atumiki kumusi uko. Iwo anawakana atumiki.

¹²⁴ Monga kadzutsa wa Billy Graham, pamene iye anali mu mzinda wathu, mu Louisville, Kentucky. Ine ndinali pa kadzutsa wake. Iye anati, “Ine ndimapita mu mzinda,” iye anati, “Ine . . .” Iye ananyamula Baibulo. Iye ndi wokhulupirira wamkulu mu Baibulo. Iye anati, “Ine ndimapita mu mzinda ndipo ndikukakhala ndi—msonkhano, ine ndikukhala ndi otembenuka sarte sauzande, kapena zigamulo.” Iye anati, “Ndipo ine ndikudzabwerera, miyezi sikisi kuchokera pamenepo, ine sindingathe kukapeza sarte.” Ndipo iye anati, “Paulo anapita mu mzinda ndipo anamtembenuza mmodzi, ndipo pamene iye anabwererako, chaka chotsatira, wotembenukayo anali atatembenuza, otembenuka kuchulukitsa otembenuka, mpaka iye anali ndi mahandiredi a otembenuka mwa mmodzi ameneyo.” Iye anati, “Tsopano chavuta ndi chiyani?” Iye anati, “Inu gulu la alaliki aulesi.” Iye anati, “Inu mumakhala ndi mapazi anu ali pamwamba pa desiki, ndipo osapita uko ndi kukawachezera anthu amenewo.”

¹²⁵ Tsopano kodi ndine ndani, munthu wosaphunzira ngati ine, kuti ndizitsutsana ndi mvangeli wamkulu? Koma ine ndikanakonda ndikananena mawu amodzi kwa iye. “Billy, mlaliki amene anatenga wotembenuka wa Paulo.” Mukuona?

¹²⁶ Chinali chifukwa chakuti Paulo anamutengera iye mwakuya mokwanira, kuti Khristu anabwera mwa iye ndipo iye anali Moto wamoyo, mpaka pansu ku Kukhalapo kwamoyo. Osati kusuntha kwina kwaluntha, kapena wojowina wina, kapena kutenga cholemba china chisainidwe, kapena kulonjeza kuti iye abwera ku tchalitchi. Mutengereni iye ku ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo mukatero iye adzatero—iye adzakhala pa Moto, iye adzabala ana. Iwe ungachite bwanji zimenezo pamene iye ndi wosabala? Iye sangakhoze kukhala ndi ana pokhapokha iye atakhala nawo Moyo iyemwini. Ndipo ndiyo njira yokhaya imene chirichonse chingakhoze kudzilengezanso chokha, ndi mwa nyongolosi. Ndipo nyongolosi ndi Mzimu Woyera umene unali mwa Khristu, uli mwa wokhulupirira.

¹²⁷ Tsopano ife tikuzindikira, chizindikiro chotsiriza cha Mulungu kwa Abraham, kwenikweni, chinali Mulungu, Mawu. Kumbukirani, Mulungu Mawu olonjzedwa amene anali atalonjzedwa kwa iye nthawi yonseyi, anayankhula kwa iye mu thupi la munthu. Mwamuna atayima pamenepo, akuyankhula ndi iye, kuzindikira malingaliro amene anali

mu mtima wa Sarah; ndipo iye, kumbuyo kuseri kwa Iye, mu hema. Chimenecho chinali chizindikiro chotsiriza. Zindikirani tsopano. Iye anali atawonekera kale kwa iye, mu zophiphiritsa zambiri, ndi zina zotero, monga kuwala, ndi—ndi moto, ndi zina zotero, anawonekera kwa iye, koma tsopano zindikirani. Ndipo nthawi yomweyo . . .

128 Ine ndikufuna kuti inu muzindikire chimene chinachitika kwa banja lakale. Tsopano ine ndikuyembekeza inu simundiwerengera ine ngati wosadalirika. Ndipo—ndipo ngati inu simukukhulupirira izi, ingozisiyani izo zokha, basi, mwaona. Koma ine ndikungofuna kuti ndikuuzeni inu chimene ine ndikuganiza chinachitika.

129 Kodi inu munazindikira tsopano, momwe Sarah adzakhalire ndi mwana uyu? Tsopano iye ndi wa usinkhu wa zaka handiredi. Tsopano wina akuti, “Chabwino, izo zinali zosiyana ndiye.” Baibulo linati chiberekero chake chinali chakufa, ndipo Baibulo linati iwo onse anali ogonja-bwino mu usinkhu.

130 Koma Iye akuchita kwa Sarah ndi Abraham, akubwera cha kumeneko, monga momwe Iye analonjezera kudzachita kwa Mbewu yawo. Ndipo Iye anachita izo! Ine ndikhoza kutsimikizira zimenezo, ndendende basi masitepe omwe Abraham anatenga. Tsopano tayang’anani pamene iye ali pano tsopano pamene Mulungu uyu anabwera ndipo anayankhula kwa iye, mu thupi laumunthu, anadzizindikiritsa Yekha kwa iye. Nthawi yomweyo tsopano . . .

131 Kodi Sarah adzakhala bwanji ndi mwana ameneyu? Tsopano Abrahamu anali atakhala ndi mkaziyo, ndipo mwinamwake iye anali . . . Iwo anati, “Thupi lake linali ngati lakufa.” Baibulo linati ilo linali. “Thupi lake tsopano lafa. Mimba ya Sarah yafa. Koma iye sanadzandime. Komabe, iye anakhulupirira izo.” Tsopano penyani, ngati Sarah . . .

132 Ine ndiri mwa omvetsera osakanikirana, ndipo inu mundikhululukire ine, alongo. Ndipo inu mumamvetsera kwa dokotala wanu; ndipo ndine m’bale wanu. Koma tsopano zindikirani. Sarah, ali ndi zaka nainte, ndi wokalamba kwambiri kuti apite mu kubereka. Mtima umenewo sukanapirira izo. Inu mukudziwa zimenezo. Ndipo chinthu china, mitsempha yake yamkaka inali itawuma. Iwo analibe mabotolo athanzi ndi aukhondo mmasiku amenewo. Mwaona, amayenera kukhala mayi wonyowa. Zindikirani. Kotero kodi Iye achita motani zimenezo? Iye akhala bwanji ndi mwana uyu? Mimba yake yafa. Iye wafa mu thupi lake, iyemwini, ndipo Abraham anafa.

133 Inu mukudziwa chimene Iye anachita? Iye anawasintha iwo. Iye anawabwezeretsanso iwo kukhala mnyamata ndi mtsikana. Ine ndikhoza kutsimikizira zimenezo. Iye anawapanga iwo kukhala mnyamata ndi mtsikana, anawabwezeretsanso iwo kukhala achichepere. Oh, ndi lonjezo lodabwitsa bwanji!

Inu mukuti, “Oh, M’bale Branham!”

¹³⁴ Chabwino, ingodikirani miniti yokha. Musati... Ingogwiritsitsani. Izi zikhoza kupweteka pang’ono pokha, kwa azamalamulo, koma ine—ine ndikufuna inu mwone izi tsopano kwa miniti yokha. Tsopano ife tikungophunzitsa monga phunziro la Sande sukulu pa izi. Iye anawasandutsa iwo kukhala mnyamata ndi mtsikana kachiwiri, pafupifupi zaka twente zakubadwa.

¹³⁵ Abraham, tsopano taonani, iye wakalamba. Ndevu zake zikulendewera pansi. Thupi lake linali ngati lakufa. Mikono yake yaying’ono, yakale yonyeka. Sarah, shawelo yaing’ono pa phewa lake ndi kachipewa kakang’ono kwambiri, agogo aakazi aang’ono akugwedezeka poyenda ndi ndodo.

¹³⁶ Ine ndikhoza kuwona mmawa wotsatira. Bwanji, Abraham ali ndi nthumbira yaikulu ku nsana kwake, tsitsi loyera likugwera pansi. Ndipo Sarah anati, “Abraham, wokondedwa, bwanji, zako—ndevu zako zada.” “Bwanji, Sarah, nso okongola awo akuwala monga momwe iwo amachitira nthawizonse. Masaya ako ali ndi duwa mwa iwo.” Dzuwa lisanalowe usiku wotsatira, iye anali atabwerera kwa mtsikana, ndipo iye anali kwa mnyamata.

Inu mukuti, “Zamkutu, M’bale Branham!”

¹³⁷ Oh, inde, izo zinali, nazonso. Onani tsopano lonjezo lodabwitsa ndi choyimira cha Mbewu yachifumu ya Abrahamu, ikubwera mwamsanga. Kumbukirani, kodi ilo ndi lonjezo? Inde, ife tidzasinthidwa. Iwo anasinthidwa kukhala mnyamata ndi mtsikana, kungosonyeza ndendende zomwe Mpingo, Mbewu yachifumu, iti idzachitiridwe.

Inu mukuti, “Kodi limenelo ndi lonjezo?”

¹³⁸ Atesalonika Woyamba 4:17, “Lipenga la Mulungu lidzawomba, ndipo ife tidzasinthidwa mu kamphindi, mu kuthwanima kwa diso, kukwatulidwira mmwamba limodzi.” Chifukwa chiyani? Thupi lake, matupi awo, ankayenera kusinthidwa kuti alandire mwana. Ndipo matupi athu achivundi, oyipa adzayenera kuti adzasinthidwe, kuti adzalandire Mwana, chifukwa ife tidzakwatulidwira mmwamba. Ife tidzayenera kudzakhala thupi losiyana ndi ili, pakuti ife tidzakwatulidwira mu mlengalenga, kuti tikakomane naye Iye. Amen. Palibe ku-... Kulondola basi ndi Malemba, inu mukuona. Iwo anasinthidwa. Ngati ife tidzakumane konse ndi Ambuye mu mlengalenga, ife sitingakhoze kukumana naye Iye ndi mtundu uwu wa thupi, chifukwa ndife omangidwa kudziko lapansi. Koma ife tidzalandira limodzi, aleluya, limene liti lidzapite mmwamba mu Mkwatulo.

¹³⁹ Ndipo gawo lokongola la izo, izo ziri pafupi kwambiri. Ife tikuwona zizindikiro zonse zikukhala molondola. Sipatenga

nthawi yayitali tsopano, limodzi la mmawa uwu padzakhala kusintha. Mukuona?

¹⁴⁰ Koma, kumbukirani, izo zidzangobwera kwa Mbewu yachifumu imeneyo yokha. Kubwera kwa Yesu kudzakhala kwachinsinsi kwambiri, anthu ena onse sadzadziwa kanthu za zimenezo. Kodi inu mukudziwa, iwo mwinamwake sadzakhala ambiri. “Monga izo zinakhalira mmasiku a Noah, pamene miyoyo eyiti inapulumutsidwa ndi madzi, chomwechonso zidzachitika mu kudza kwa Mwana wa munthu.” “Khwalala ndiro chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza, koma ochepa iwo adzakhala amene ati adzayipeze iyo.” Inu mukuti padzakhala mamillioni kumeneko; eya, monse kudutsa mibadwo, owomboledwa, ndithudi. Koma, malo Okwatulidwira awo, pamene ife taima tsopano!

¹⁴¹ Kodi ndi chiyani chidzachitike limodzi la masiku amenewa? Iwo adzanena kuti, “Tsopano, inu mukudziwa, ife tiri pano mu nthawi ya Chisawutso. Ine ndimaganiza kuti Mpingo uyenera udzakwatulidwe nthawi ya Chisawutso isanafike.” Icho ndi Choonadi. Osati mpingo; Mkwatibwi. Mpingo ukudutsa mu nthawi ya Chisawutso, koma osati Mkwatibwi. Ayi, bwana. Iye wawomboledwa. Iye alibe kanthu koti ayeretsedwe nako. Iye ndi wangwiro kale. Mzimu Woyera wabwera mwa Iye ndipo wadzamuyetsa Iye, ndipo wadzachotsa zonyansa zonse ndi uve wa mdziko, ndipo Iye akuwakhulupirira Mawu amenewo ndipo wadzakhala gawo la Iwo. Uko nkulondola. Popanda Mzimu Woyera, palibe chochita. Ndi Mkwatibwi akutuluka mu mpingo. Ndipo pamenepo, iye, amene amatchedwa “wotsalira wa mbewu ya mkazi,” akusiyidwa kuti adutse nthawi ya Chisawutso.

¹⁴² Inu mukudziwa, nthawi ina pambuyo pa Malemba onse, Yesaya, Malaki 3, ndi Yesaya 40, akulosea za kudza kwa Yohane Mbatizi, Yohane anabwera basi ndendende mu mzere ndi Malemba amenewo. Ndipo ngakhale ophunzira anabwera kwa Yesu ndipo anati, “Ndi chifukwa chiyani Alembi, Malemba, amanena kuti Eliya ayenera kubwera poyamba?”

¹⁴³ Iye anati, “Iye anabwera kale, ndipo inu simunadziwe izo. Iye wabwera, ndipo iwo anamuchitira iye ndendende basi zomwe izo zimayenera kudzachita, ndipo inu simunazidziwe izo.”

¹⁴⁴ Tsopano, ilo likhoza kukhala limodzi la masiku awa, inu mukhoza kunena kuti, “Nanga bwanji Mkwatulo?”

¹⁴⁵ “Iwo wadutsa kale, ndipo inu simunadziwe izo.” “Padzakhala awiri pa bedi; mmodzi adzatengedwa, mmodzi adzasiyidwa.” Inu mukudziwa, alipo pafupifupi mahandiredi angapo a anthu omwe amasowa pa dziko lapansi, tsiku lililonse, mulimonse, inu mukudziwa. Iwo sangakhoze kuzifotokoza izo.

¹⁴⁶ Ndipo tangoganizani za zimenezo, zachisoni, kuti anthu azidzapitirira kumalalikirira, ndi kumakhulupirira kuti iwo akupulumutsidwa.

147 Ndipo Nowa analowa mu chombo, ndipo chitseko chinatsekeka kumbuyo kwake ndi dzanja la Mulungu. Dzuwa linatuluka, ndipo linakalowa, masiku seveni chirichonse chisanachitike. Ndipo anthu anapitirira kumalalikira, kupitirirabe kumaseka, ndi china chirichonse, osadziwa kuti chifundo chawo chokha chimene iwo anakhala nacho chinatsekedwa kwa iwo.

148 Taganizani, atumiki adzakhala akuphunzitsabe alaliki ndi kumawakhazikitsa iwo, ndi zinthu monga izo zikuchitika, mpingo ukupitirirabe; ndipo wopanda chifundo kwathunthu, wopanda kanthu, kudulidwa kwathunthu; Mkwatulo wapita. “Msiyeni iye amene ali wodetsedwa akhale chiyipirebe,” Lemba limanena zimenezo. “Anabwera kale ndipo inu simunadziwe izo.” Taganizani za zimenezo, usikuuno, abwenzi, ndipo penyani zimene zikuchitika.

149 Palibe kalikonse mdziko kamene kangakutonthozeni inu tsopano koma Mawu a Mulungu. Mukuona? Palibe chiyembekezo china; fuko lanu, palibe pena paliponse.

150 Ife tadyedwa ndi mbozi mpaka kumapeto. Inu mukudziwa zimenezo. Chikominsi chadya nyongolosi chinthucho. Izo ziyenera...Izo ziyenera kukhala mwanjira imeneyo. Inu simudzaziletsa izo. Baibulo linati izo zikanadzakhala mwanjira imeneyo, kotero inu simudzadzilepheretsa izo basi. Ndizo zonse.

Konzekeerani Mkwatulo. Ndicho chinthu chokhacho choti muchite.

151 Atesalonika, a—Atesalonika Woyamba 4:17 ananena kuti, “Ife tidzasinthidwa,” monga Abrahamu anachitira, “ndi kutengedwera mmwamba,” thupi losinthika. Tsopano, Abrahamu, matupi awo akale ankayenera kusinthidwa. Chomwechonso athu adzayenera kusinthidwa, kuti akwaniritse lonjezo. Ife tidzayenera kusinthidwa. Tsopano, inu mukuti, matupi akale awa. Ine ndikufuna kuti. . .

152 Ine ndinali kuyankhula ku Kiwanis, kuno nthawi ina kalelo. Ndipo a—ndipo dokotala anatuluka, pambuyo pake, ndipo iye anati, “Bambo Branham,” anati, “Ine ndimayamikira kuyankhula kwanu, koma,” anati, “inu mukudziwa, ine sindingakhulupirire kuti—kuti—kuti, chirichonse, pokhapokha izo zitatsimikiziridwa mwasayansi, za kubadwa kwa namwali kuja ndi zinthu monga zimenezo, ndi za kukhala Mulungu.”

153 Ine ndinati, “Chabwino, inu simudzamukhulupirira konse Iye, chifukwa inu simungakhoze kutsimikizira Mulungu mwasayansi. Inu muyenera kumukhulupirira Iye mwa chikhulupiriro, mwa chikhulupiriro.”

Iye anati, “Chabwino, ine sindimakhulupirira chirichonse chomwe sichiri sayansi.”

Ine ndinati, “Kodi ndinu mwamuna wokwatira?”

Iye anati, “Inde, bwana.”

Ine ndinati, “Kodi inu mumamukonda mkazi wanu?”

Iye anati, “Ine ndithudi ndimatero.”

154 Ine ndinati, “Mwasayansi ndiwonetseni ine chomwe chikondi chiri ndiye. Ine ndikufuna kugula china, ngati inu mungakhoze kundiuza ine kogulitsira mankhwala kumene amagulitsa icho. Ine ndikuchifunadi icho.” Ine ndinati, “Ine . . .” Mwaona, chinthu chophweka basi.

155 Ine ndinati, “Ine ndikufunsani inu funso. Tsopano, apa, kodi ife tinapangidwa kuchokera ku fumbi la dziko lapansi?”

Iye anati, “Inde, bwana.”

156 Ine ndinati, “Ife timalandira fumbi limenelo pa kudya chakudya chimene chimachokera ku nthaka, ndipo icho ndi moyo wa zomera, ndi zina zotero.”

157 Inu mukuona, inu mukhoza kukhala moyo ndi chinthu chakufa chokha. Mukuona? Ngati inu mukhala moyo, chinachake chiyenera kufa kuti inu mukhoze kukhala moyo, mwathupi. Ngati inu mukudya mbatata, iyo inafa. Ngati mukudya ng’ombe, ng’ombeyo inafa. Ngati mukudya nkumbaba, nkumbayo inafa. Ngati mukudya zamasamba, izo zinafa. Ndi mtundu wa moyo. Ndipo inu mumangokhala moyo, mwachibadwa, mwa—ndi chinthu chinachake chakufa. Zinthu zakufa! Tsopano izo sizikungokhala nkulingalira, mzanga, kuti inu mungakhoze kokha kukhala Wamuyaya ndi chinthu chinachake chimene chinakuferani inu? Khristu anafa, inde, anauka kachiwiri, kuti adzatsimikizire Umulungu Wake. Zindikirani tsopano.

158 Ine ndinati, “Dokotala, ngati ine ndidya chakudya ndiye, nthawi iliyonse imene ine ndikudya chakudya, icho chimalowa mthupi langa ndipo icho chimapanga makhungu a magari.”

Iye anati, “Uko nkulondola.”

“Ndiye nthawi iliyonse imene ine ndidya, ine ndimakonzanso moyo wanga.”

Iye anati, “Ndiko kulondola, makhungu atsopano a magari.”

159 Ine ndinati, “Ine ndikufuna ndikufunseni inu chinachake ndiye. Pamene ine ndinali ndi zaka sikisitini, ine ndimadya chimanga ndi nyemba ndi mbatata ndi nyama, monga momwe ine ndikuchitira tsopano. Ndipo nthawi iliyonse ine ndikadya, ine ndimakula ndi wamphamvu. Ndiyeno pamene ndinafika pafupifupi usinkhu wa zaka twente-thuu, munthu aliyense, ziribe kanthu momwe iwe umadyera, momwe umadyera bwino, iwe umakhala ukukalamba ndi kumafowokera. Tsopano ngati ndikutsanulira madzi kuchokera mu kapu *iyi*, kuthira mu *iyi*, ndipo nkuthira theka yodzaza; ndiyeno nkumangopitiriza kumathira, nditatha kudzadzitsa theka kudzadza; ndipo mmalo

momakwera mmwamba, iwo nkumapita pansi. NditSIMIKIZIRENI ine mwasayansi momwe izo zimachitikira. Mukuona? Zimakhala bwanji kuti ine ndikudya chakudya chomwecho, ndikukonzanso moyo wanga tsiku lililonse, molingana ndi. . . Zimatsimikizira, mwasayansi zikutsimikizira kuti ine ndikukonzanso moyo wanga pamene ine ndikutenga makhungu atsopano a magari, mtundu womwewo wa magari umene ine ndinatenga pamene ine ndinali ndi zaka sikisitini zakubadwa. Koma zimatheka bwanji zimenezo, ine nditafika pafupifupi twente chakuti ndi chinachake, ndiye ziribe kanthu kuti ndikudya zochuluka bwanji, Ine ndikutsikira pansi, kukalamba ndi kukalamba ndikukulirapo, ndi kumangotsikira pansi nthawi zonse? Mmalo mondizaza ine, monga izo zinachitira pamenepo, tsopano izo zikundigwetsera ine pansi.” Kumeneko ndi kukoza zokumana. Ndicho chimene icho chiri.

¹⁶⁰ Koma Mulungu anapanga chithunzi, ndipo Iye anakupezani inu pamene inu munali pafupifupi usinkhu wa zaka twente ndi chinachake, ngati palibe chomwe sichinasokoneze monga mnyamata wamng’ono wolumala wakhalapayay. Izo ziri ngati a—phesi la chimanga linayambapo, ndipo chinachake chinadzagona pa ilo ndi kulipangitsa ilo kumera mokhota; ngati mungakhoze kusuntha chinthu chokhota chija chimene chinachipangitsa icho kuchita zimenezo, phesilo lidzawongoka. Iye ayenera kutero. Ndizo zonse. Zindikirani, ngati palibe chosokoneza icho, ndi zimenezotu pamenepo, dona wabwino wamng’ono, mnyamata wabwino wamng’ono. Inu ndi amuna anu mutaima pamodzi, Adamu wamakono ndi Eva kuyambira pachiyambi. Mulungu anati, “Ndi awo pamenepo. Tsopano imfa iwe—iwe uwatsatire iwo. Iwe ukhoza kuyamba kuwatenga iwo, koma iwe sungakhoze kuwatenga iwo kwathunthu mpaka Ine nditaitana.” Tsopano ndi chiyani chimenecho? Ndi chithunzi chosatsukidwa. Oh, mai! Mukuona?

¹⁶¹ Ndizo ndendende zimene Iye anachita kwa Sarah ndi Abraham. Iye anachotsapo ukalamba. Ukalamba ndi chizindikiro cha imfa. Ndipo sikudzakhala zizindikiro za imfa Kumwamba. Mwaona, kukumbukira konse kwa imfa kudzachotsedwapo, ndipo sikudzakhalako ukalamba. Ife tonse tidzakhala achichepere. Ndi chithunzi chabe chimene Mulungu anajambula mu unyamata wanu. Ndipo tsopano Mulungu anatenga ndipo anamukhazika Abraham ndi Sarah kubwerera ku usinkhu wabwino wachinyamata umenewo kachiwiri, koteru ndi ife pamenepo.

¹⁶² Ndipo umboni wina womwe ine ndikufuna ndikuwonetseni inu tsopano. Ine—ine sinditero. . . Ine ndikumverera kuti izo sizikuyenda bwino kwambiri. Ine ndikungoyenera kutero. . . Inu simukukhulupirira zimenezo. Chabwino, ndiloleni ine ndikufunseni inu. Ndiroleni ine ndikuwonetseni inu chinachake. Ndiroleni ine ndikusonyezeni inu kuti iwo anachita izo. Tsopano

penyani.

¹⁶³ Tayang'anani kumene iwo anali, pa mapu, pamene Mulungu anawonekera kwa iwo, kumtunda uko pafupi ndi Sodomu. Mwamsanga pambuyo pake anayenda ulendo wa pafupifupi mamilosi firii-handiredi kumapita ku Gerari. Umenewo ndi ulendo wautali ndithu kwa mwamuna ndi mkazi wokalamba. Apa pali bambo wachikulire uyu tsopano, ndevu zake zikulendewera pansu, ali pa ndodo yake. Apa pali agogo aakazi, inu mukudziwa, atavala chipewa chaching'ono, akunjenjemera kumbuyo kwake, akupanga masitepe a mainchesi foro kapena faivi pamene iye akupita.

¹⁶⁴ Ndiyeno, vuto lake linali, pamene iwo anakafika ku Gerari, kumeneko kunali Abimeleki, mfumu inali kufunafuna wokondedwa. Ndipo akazi abwino onse awo amene iye anali nawo kumeneko, atsikana Achifilisti; pamene iye anamuwona Sarah, iye anamukonda iye, ankafuna kuti amupange iye akhale mkazi wake. Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ha-ha! Oh!

¹⁶⁵ Oh, m'bale, Baibulo liri ngati kalata yachikondi. Iwe umayenera kuliwerenga pakati pa mizere, kuwona chomwe Ilo likutanthauza. Mulungu anati, "Iye anazibisa Izo kwa maso a anzeru ndi aluntha, ndipo anaziulula Izo kwa makanda amene akanati apunzire."

¹⁶⁶ Pamene ine ndiri kunja ku mishoni, mkazi wanga amandilemba ine kalata. Ndipo ine ndimamukonda iye, ndipo iye amandikonda ine. Ndipo iye amati, "Wokondedwa Bill, usikuuno ine ndangowagoneka kumene ana. Ine ndinagwira ntchito lero." Ine ndikuwona zomwe iye akuwerenga, zomwe iye akulemba. Koma, onani, ine ndimamukonda iye kwambiri, ine ndikhoza kuwerenga kumene pakati pa mizere. Ine ndikudziwa zimene iye akunena. Iye samasowa kuti achite kundiuza ine. Ine ndikudziwa, chifukwa ine ndimakhoza kuwerenga pakati pa mizere.

¹⁶⁷ Umo ndi mmene zimakhallira ndi Mulungu, pamene osati kuyesetsa kuwerenga ku nyuzipepala ina, kayimidwe kena ka fioloje, koma kugwa mu chikondi ndi Iye. Kukhala pansu ndi kumutengera Iye kwenikweni mu mtima wako, "chikondi cha Mulungu chikutsanulidwa mu mtima wawo mwa Mzimu Woyera," ndiye nkuyamba kuwerenga Baibulo ndipo iwe umadzaliwona Ilo likubwera pakati pa mizere. Mwaona, iwe umadziwa chimene Iye akunena. Iye sananene konse izo momveka m'Mawu. Yesu anawayamika Atate chifukwa chakuti Iye anali "atabisira zinthu zimenezo pamaso pa anzeru ndi aluntha." Tsopano, palibe wina aliyense amene angawerenge makalata a mkazi wanga monga chomwecho, chifukwa ine ndimamukonda iye mwanjira imeneyo, mwaona, ndipo umo ndi momwe iye amandilemba ine. Umo ndi momwe

Mulungu amalemba kwa inu. Izo ziri pakati pa mizere, iwe ukuziwerenga Izo.

¹⁶⁸ Apa iye ali tsopano, Sarah, ndithudi, anapita kumusi uko. Kodi inu mungalingalire agogo aakazi aang'ono, inu mukudziwa? Ndipo atsikana onse okongola amenewo kumusi uko mu—mu gulu la Afilisti, mdziko la Gerari. Ndipo apa pali Abimeleki pamenepo, iye ndi mfumu yachichepere yowoneka bwino, ndipo iye akufuna kuti azipezere wokonedwa, kotero iye akuyang'ana pozungulira ponse. Iwo ndi okongola, ndi chirichonse. Koma iye akuwona agogo akubwera, inu mukudziwa, akunjenjemera, amanjenje, akubwera pamenepo, iye anati “Ndi amene ine ndimawayembekezera. Ndiye iye!” Anati, “Oh!”

¹⁶⁹ Ndipo Abraham anati, “Ine ndikukupempha iwe, Sarah, uwonetse kukoma mtima uku kwa ine. Ndiwe wokongola pokuyang'ana, iwe ukudziwa.” Anati, “Pamene ukafike kumeneko, iwe ukati ine—ndine mchimwene wako, ndipo ine ndikanena kuti ndiwe mlongo wanga. Chifukwa, ngati suteru, iwo akandipha ine ndi kukutenga iwe.”

¹⁷⁰ Mwaona, sizimatheka kukhala ndi akazi awiri nthawi imodzi nthawi imeneyo, mwaona, kotero ndiye ife. . . Iye sakanakhoza kukhala ndi amuna awiri, kani, pa nthawi imodzi. Limodzi la masiku awa, ine ndidzalalikira pa zimenezo. Ndiye, iwe ukayankhula za *Mbewu ya Serpenti* kukondoweza chinachake, inu mudikirire mpaka izi zitadzatulukira. Chiyani—chiyani, tsopano? Kumbukirani.

¹⁷¹ Ndiye ife tikupeza kuti pamene tinawona izo zikubwera, agogo aakazi achikulire monga choncho, Abimeleki anagwa mu chikondi ndi iye, ndipo anapita ndipo anakamutenga iye kuti akhale mkazi wake.

Taganizani za zimenezo. Mwaona pamene Iye anawasandutsa iw kubwerera mmbuyo? Ndithudi, Iye ankayenera kutero.

¹⁷² Baibulo ili, kalata ya chikondi, ndi chinachake chimene Mulungu amatilemba ife. “Iye wazibisa Izo kwa maso a anzeru ndi aluntha, ndipo Iye adzadzizulula Izo kwa makanda omwe angaphunzire.” Iye amabisa. . .

¹⁷³ Iye anabisa kudza Kwake. Iye anamubisa Yesu kwa Afarisi, ophunzira aja a Lemba. Ife tiribe chirichonse ngati iwo lero. Ziribe kanthu momwe iwo analiri ophunzira, iwo sanamuzindikire Iye. Iye anabisidwa. Baibulo linati Iye anali.

¹⁷⁴ Ndipo, inu mukudziwa, Baibulo linati azibusa a tsiku lino akanadzabisidwa mwanjira yomweyo. “Ammutu, amalingaliro apamwamba, okonda zosangalatsa kuposa kukonda Mulungu, okuswa chigwirizano, onenera zabodza, osadzigwira, ndi onyoza amene akulondola. Okhala ndi a . . .”

Inu mukuti, “Ndiwo achikominsi.” Ayi, ayi.

175 “Akukhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana Mphamvu yake; kwa otere chokaniko.” Mwaona? Uko nkulondola. “Uwu ndiwo mtundu umene umapita nyumba ndi nyumba, ndi kutsogolera akazi opusa olemedwa ndi zilakolako zosiyanasiyana,” zina zotero. Zindikirani.

176 Tsopano ife tikumupeza Abrahamu kumusi uko. Ndipo Abimeleki anafika, anati, “Ndi mmodzi amene ine ndimamuyembekezera, nthawi zonsezi.” Kotero iye anali ndi atsikana ake kuti abwere kudzamutenga iye ndi kumutengera iye kunja uko, ndipo, oh, mwinamwake kumukonza iye zonse, ndi kumupanga iye kuwoneka ngati mfumukazi ya mtundu wina. Ndipo usiku umenewo. . .

177 Ine ndikufuna inu muzindikire apa chisomo cha Mulungu kwa mneneri Wake. Izi zikhoza kutsamwitsa pang’ono pokha, koma ndi Choonadi. Ziribe kanthu momwe Izo zikuwonekera, inu muyang’ane pa izi zomwe Baibulo linanena.

178 Tsopano ine ndikukhoza kumuwona Abimeleki, iye akuganiza, “Mawa ine ndimukwatira mtsikana wokongola wa Chihebri uyu. Ndipo iye ali mzipinda za uko tsopano, ndipo adzakazi anga akumukonza iye ndi kulikongoletsa tsitsi lake, ndi kuzikonza zonse.” Tsopano kodi inu mungalingalire mkazi wachikulire wa usinkhu wa zaka nainte akudzikonzekeketsa wanga choncho, kuti akwatiwe ndi mfumu wachichepere? Kotero ife tikupeza, pamene iwo akumukonza mtsikana wokongola wa Chihebri uyu, ndipo iye akusamba ndi—ndi kugona pansu, ndi kutambasula mapazi ake, atatha kunena mapemphero ake, ndipo anagona, anati, “Oh, mai!”

179 Tsopano kodi inu mungalingalire Abraham akuchita chinyengo choterocho, mwamuna yemwe ananena chinthu chonga icho chokhudza mkazi wake? Kunena za munthu wamantha! Abraham anachita zimenezo. Ndipo apo iye wakhala kunja uko tsopano, atatha kuchita chinthu chonga chimenecho. Zindikirani.

180 Ndipo Abimeleki, usiku umenewo Ambuye anawonekera kwa iye, mu loto, ndipo anati, “Ndiwe basi uli ngati munthu wakufa.” Anati, “Iwe watenga mkazi wa mwamuna wina.”

181 Iye anati, “Ambuye, Inu mukudziwa kukhulupirika kwa mtima wanga.” Anati, “Ine—ine. . . Iye anandiuza ine ameneyo anali wake—mchimwene wake, ndipo iye anandiuza ine kuti uyo anali mlongo wake.”

182 Iye anati, “Ine ndikudziwa kukhulupirika kwa mtima wako, ndi chifukwa chake ndakuletsa iwe kuti usandichimwire Ine. Mukuona? Koma uyo, mwamuna wake, ndi mneneri Wanga.” Tayang’anani pa chisomo Chake kwa mneneri Wake, ngakhale iye anali mu kulakwitsa. Mukuona? Anati, “Iye ndi mneneri Wanga. Ine sindimva mapemphero ako. Iwe upite ukamubwezere

mkazi wake, ndipo ukamulole iye akakupempherere iwe. Ngati suteru, fuko lako lonse lapita,” chiberekero chirichonse chinali chitasekedwa. Taganizani za zimenezo. Ndizo ndendende zimene Iye ananena. Ndipo Abimeleki anali munthu wabwino, ndipo ankamuwopa Mulungu. Inde, bwana.

¹⁸³ Koma inu mukuona chimene chisomo cha Mulungu chimachita? Apo panali mneneri Wake kunja uko, yemwe anamupereka mkazi wake kuti akwatiwe kwa mwamuna wina, komabe akuyembekezera lonjezo la mwanayo, ndi zinthu monga zimenezo, ndipo chisomo cha Mulungu chimakhala ndi Mawu amenewo mosalabadira chomwe izo ziri. Uko nkulondola.

¹⁸⁴ “Mwamuna wake ndi mneneri Wanga. Ndipo Ine sindimva pemphero lako. Ziribe kanthu momwe uliri wolungama, ndi momwe uliri wabwino, ndi momwe iwe uliri wanzeru; kupatula ngati iye atakupempherera iwe, ndiwe munthu wakufa.” Chotero iye anatenga ndipo anakamubwezera Sarah. Oh, mai!

¹⁸⁵ Ndiye Isaki anabwera powonekera. Tsopano potseka, mwamsanga tsopano ine ndikufuna kuti ndikupezereni inu chinachake. Isaki anabwera powonekera ndipo zitatero lonjezo linakwaniritsidwa.

¹⁸⁶ Tsopano Isaki atabwera, mnyamata wamng'onoyo anali atafika pafupifupi usinkhu wa zaka thwelovu, zina zotero, Mulungu anapanga mayesero awiri a Abraham. Iye atamuyesa kale Iye, kwa zaka twente-faivi tsopano, ndiye Iye anapanga mayesero apawiri. Tsopano Iye anati, “Abraham, ine ndifuna kuti utenge mwana wamwamuna uyu tsopano, mwana wako mmodzi yekhayo, ndipo umutengere iye ku phiri limene Ine ndikusonyeze iwe pano mmasomphenya awa, ndipo Ine ndikufuna iwe umutengere iye kumeneko ndi kukamupereka iye kwa nsembe.”

¹⁸⁷ Ndipo Iye anati iye sanakane—sanakane konse kuchita zimenezo. Iye anangodzuka, mmawa wotsatira Ambuye atatha kuyankhula kwa iye, anakwera mphongolo zazing'onozo ndipo anatenga nkhu zina ndi zinthu, ndipo anazigawaniza izo, ndipo anyamuka ndi mphongolozo. Iye anayenda masiku atatu, ndipo kenako anafika pamalowo, iye anayang'ana kutali pa mtunda wautali, atatha kuyenda masiku atatu. Tsopano apa ndi pamene Abraham anali, ndi ulendo wa masiku atatu. Ndipo pamene munthu nthawi imeneyo analibe mapazi a mafuta monga ife tiri nawo lero, ndipo munthu wamba aliyense akhoza kuyenda mailosi twente-faivi pa tsiku. Mukuona? Kodi iye anakafika kuti, uko mu nkhalango imeneyo?

¹⁸⁸ Ndipo iye anati, “Tsopano inu mudikire apa.” Ine ndimakonda izi za Abraham. Iye anati kwa antchitowo, anati, “Inu mudikire pano ndi mphongolo, ndipo ine ndi mwana wanga tipita kutsidyako kukapembedza, ndipo ife tidzabwerera.”

189 Kodi iye akachita motani zimenezo, pamene iye anapita uko kuti akamuphe iye? Mulungu anamuza iye, anati, “Pita uko ndipo ukatenge moyo wake.”

190 Koma kodi Baibulo linanena chiyani, mu Aroma 4? “Abrahamu anadziwa kuti iye anali atamulandira iye monga mmodzi wochokera kwa akufa, ndipo anali wokakamizika kwathunthu kuti Mulungu anali wothekera kumudzutsa iye kwa akufa, kuchokera kumene iye anamulandira iye ngati chithunzi.” Mukuona?

Anati, “Inu mudikirire apa.”

191 Momwe izo zingakhalire, ine sindingakhoze kukuuzani inu. Kodi inu mungaganizire za mlongo uyo ali ndi mwana mmanja mwanu, ndi amayi akhala mu chikuku, mnyamata wamng’ono pamenepo, adadi cha kuno? Ine sindikudziwa momwe Iye ati achitire izo. Ine sindikudziwa basi momwe Iye ati achitire izo. Koma Iye achita izo chifukwa Iye analonjeza kuti Iye akanadzatero, pa maziko akuti inu mukhulupirira izo. Iye amachita izo kwa ena. Mukuona?

192 “Mnyamata uyu ndi ine, mnyamatayo ndi ine, tidzabwerera. Mwaona, inu mudikirire apa, ndipo ife tipita tikapembedze.”

193 Ndipo iye anayika nkhuhi pa Isaki wamng’ono, choyimira cha Khristu atanyamula mtanda Wake. anapita pamwamba pa phiri. Ndipo Isaki wamng’ono anayamba kukayikira, ndipo iye anati, “Atate?”

Iye anati, “Ndine pano, mwana wanga.”

194 Iye anati, “Bwanji, guwa ndi ili, moto ndi uwu, apa pali nkhuhi, koma alikuti mwanawankhosa wa nsembe?”

195 Mvetserani mawu awa tsopano ochokera pakamwa pa Abraham. “Mwana wanga, Mulungu adzadzipezera yekha mwanawankhosa wa nsembe;” Izo zikutanthauza kuti, “nsembe yoperekedwa ndi Mulungu,” *Yehova-Yire*. Mwanawankhosa woperekedwa ndi Ambuye.

196 Ndipo pamene iye anamumanga manja ake, ndikudzamuika iye pamwamba pa—pa guwa, lingalirani momwe iyo inali nthawi tsopano. Atatha kumuyembekezera iye kwa zaka twente-faivi, ndipo Mulungu anamupanga iye, kumupangitsa iye kuti awononge chinthu chokhacho chimene anachichitira umboni kwa zaka zonsezo. Iye anali chitongo pakati pa anthu, ankamuseka iye. Ndipo apa Mulungu akuti, “Uchiwononge chinthu chomwecho chimene chidzakupatse iwe chiyembekezo chokhacho chimene iwe ungate, kuti Mawu Anga akwaniritsidwe mwa iwe. Ine ndikupatsa iwe mwanayo. Iye ali ndi zaka thwelovu zakubadwa. Iwo onse amuzindikira iye, zakupangabe iwe atate wa mafuko, koma upite ukamuphe mwana wakoyo.” Kodi inu mungalingalire zimenezo?

¹⁹⁷ Mulungu akungotiwonetsa ife. Ziribe kanthu zomwe aliyense anena, kapena chirichonse chosiyana ndi Mawu amenewo, muzikana kuyang'ana pa icho. Mbewu yeniyeni ya Abraham imakhulupirira Iwo.

“Umuwononge mwana ameneyo.”

¹⁹⁸ Ndipo Abrahamu anamugoneka iye pamenepo. Inu mukhoza kulingalira, akutenga tsitsi lake laling'ono lopiringizika ndi kulipiringizira ilo mmbuyo kulichotsa pa nkhope yake. Ndipo maso ake aang'ono abulauni akuyang'ana mmwamba monga *choncho*, ndipo milomo yake yaing'ono ikunjenjemera. Akuwuwona mpeni wawukulu uwo ukutuluka kuchokera mwa abambo ake... Taganizani za bambo. Anagoneka mutu wake waung'ono mmbuyo, ndipo anakokera khosi lake mmbuyo kuti iye akhoze kumubaya iye pakhosi ndi mpeni uwu. Oh, mu kumvera kwa Mulungu! Ziribe kanthu momwe izo zinkawonekera, iye anati, “Ine ndinamulandira iye ngati mmodzi wochokera kwa akufa. Mulungu ndi wokhoza kumuukitsa iye.” Anakwezera mmbuyo mpeniwo ndipo anayamba.

¹⁹⁹ Ndipo Mzimu Woyera unagwira dzanja lake, unati, “Abraham, Abraham!”

Iye anati, “Ndine pano.”

²⁰⁰ Iye anati, “Chotsa dzanja lako.” Anati, “Ine ndikudziwa kuti iwe umandikonda Ine ndipo ukundidalira Ine tsopano, powona kuti iwe sunati nkomwe... Iwe ukanandipatsa Ine mwana wako mmodzi yekhayo.”

²⁰¹ Ndipo basi pafupifupi nthawi imeneyo, panali nkhosa yamphongo itakoledwa ndi nyanga zake, mu nkhalango, kumbuyo kwake.

²⁰² Ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu chinachake, m'bale, mlongo. Kodi nkhosa imeneyo inachokera kuti? Taonani, inu muli kumbuyo uko, ulendo wa masiku atatu kuchokera ku chitukuko, mu nkhalango, kumene kumakhala mikango, ankhandwe, ndi mitundu yonse ya agalu akuthengo ndi zirombo, ndi zinthu kumbuyo uko zikanakhoza kupha nkhosa imeneyo pakali pano. Ndipo, taonani, iye ali pamwamba kumene pa phiri kulibeko madzi. Ndipo iye anali atanyamula miyala kuzungulira pamenepo, kupanga guwa ili, ndipo nkhosa panalibe pamenepo. Koma pamene Mulungu ankafuna imodzi, apo iyo inalipo. Ndipo awo sanali masomphenya. Iye anaibaya iyo ndipo magari anatuluka mwa iyo. Iyo inafa. Mulungu anaiyankhula iyo mukukhalapo miniti iyi, ndipo Abraham anayichotsapo iyo miniti yotsatira. Mukuona? *Yehova-Yire*, “Ambuye adzadizepera Yekha mwanawankhosa.”

²⁰³ Zosatheka kuti nkhosa ikakhale kumeneko. Ngati aliyense akudziwa za nkhosa mu nkhalango, mu chipululu monga *choncho*, kumeneko kumene nyama zonse zakuthengo ndi zinthu

zolusa kutali uko zikanapha nkhusa imeneyo pakali pano. Iyo siyikanakhalapo kumbuyo uko. Ndipo apa, pamwamba pa phiri kumene kulibeko madzi, kulibe udzu kapena kalikonse pamwamba pamenepo, ndipo iye sanakhale kumene maminiti angapo izi zisanachitike. Ndipo basi pa mphindi yomwe Mulungu ankafuna nkhusa imeneyo, apo iyo inapezeka; Iye anaiyankhula iyo mu kukhalapo.

²⁰⁴ Chimodzimodzi monga momwe Iye anawonekera kwa iye kumusi uko. Elohim, Iye ankasowa thupi, Iye ankasowa thupi kuti abweremo pansu pa dziko lapansi, koteru Iye anangosonkhanitsa kuwala kwa dziko ndi mafuta, ndi zina zotero, ndipo anadalowa mmenemo. Mwaona, Iye ndi Mulungu.

²⁰⁵ Umo ndi momwe Iye adzakuchitireni inu, inu mutakhala osaposera supuni ya phulusa mu fumbi. Iye adzayankhulabe, ndipo inu mudzakhala pamenepo. Iye adzaitana dzina lanu, ndipo inu mudzayankha. Mbewu ya Abrahamu, chiyani a . . . lonjezo limenelo linakwaniritsidwa.

²⁰⁶ Zindikirani, iyo inali nkhusa. Tsopano ngati inu muli ndi utali wa miniti yokha, ine ndikufuna kuti ndifotokoze izi. Inu mukudziwa, usiku wina ine ndinazisiya izo zokha. Ine sindinayambe ndafotokozapo izo ngakhale ku mpingo wanga. Kumbukirani pamene Iye anatsimikizira nsembe imeneyo, anatsimikizira pangano limenelo kwa iye; kutenga mbuzi yaikazi, anatenga ng'ombe (ng'ombe yaikazi), ndipo anaziganga izo pakati, ndipo anatenga nkhusa. Tsopano, kumbukirani, pamene Mbewu yachifumu ya chikhulupiriro Chake, kumbukirani, iyo sinali yaikazi, iyo inali Yaimuna. Iyo inali Yaimuna, lonjezo lakwaniritsidwa. Zindikirani, nkhusa, iye; Iye, kuti akakomane ndi Mawu. Iye ndi Mawu, Nkhusa ija, osati yaikazi. Iwo anaperekedwa poyamba, kumbukirani, Genesis 15, zazikazizo; izo zinali zoyambirira kutsika; kenako iye anatenga nkhusa. Nkhusa inali yomalizira. Iye, Nkhusa, Mawu operekedwa; osati mbuzi yaikazi, bungwe, mpingo. Mukuona? Osati yaikaziyo, mpingo; koma Yaimuna, Nkhusa. Amen. Ndicho chifukwa chake Iye anabadwa mu Epulo.

²⁰⁷ Osati mu Disembala monga mpingo wa Chiroma unayikira izo, tsiku lobadwa la mulungu-dzuwa, ndi kuliyika ilo ndi Lake, kumtunda uko pa twente-faivi wa Disembala, pamene masewera awo anali kupitirira, ngati inu mwatenga—ndi . . . munaphunzira mbiri yakale ya mpingo. Ndipo inu mukumvetsa kuti iwo anaika izo pamenepo, kuzipanga izo . . . Linali tsiku lobadwa la mulungu wa dzuwa, dzuwa, pamene ilo liiyma pafupifupi bata. Sipamakhala kusingha mmenemo kwa masiku faivi, kuchokera ku Disembala twente mpaka pa twente-faivi. Iwo amamuika Mwana wa Mulungu ndi tsiku lobadwa la mulungu wa dzuwa mofanana, kunyengerera Chikristu ndi chikunja, anazipanga izo Disembala. Iye sakanabadwa pa Disembala pa twente-faivi, bwanji, ndi mapiri a chipale chofewa kumtunda uko mu Yudea.

208 Iye anabadwa monga ana a nkghosa onse. Iye anabadwa mu nyengo ya masika. Ndipo Iye ankayenera kuti abadwe pansu pa nkghosa, chifukwa Iye anali Mwanawankghosa, ndipo nkghosa zimakhala Epulo. Ndendende. Iye anabadwa pansu pa nkghosa imeneyo. Ndicho chimene Iye anali. Iye anali Nkghosa ya Mulungu. Ameneyo anali Iye kumtunda uko yemwe anatenga malo a Isaki. Ameni. Kodi inu simukuziwona zimenezo?

209 Ndi zimenezo pamenepo, kuwonetsera apa momveka, Mkwatibwi wa Mbewu yachifumu sadzaitanidwa ndi mkaziyo, mpingo, nsembe ya mbuzi yaikazi ya chipembedzo. Ayi. Koma mwa Iye, Mawu owonetseredwa a Nkghosa, pakuti Iye ndi Mawu ndi Nkghosa, ndiye. Osaitanidwa, Iye anati, osati oyitanidwa dzina la *mkaziyo* koma, “Woyitanidwa ndi Dzina Lake. Iye akanadzawatenga anthu kuchokera mwa Amitundu,” osati chifukwa cha dzina la mkaziyo, koma, “kwa Dzina Lake,” akanadzatenga Dzina Lake. Oh, mai! Kodi inu mukuziwoperanji izo, ndiye? Wamitundu akanadzatenga Dzina Lake, Nkghosa; osati dzina lake, mpingo. Osati mkaziyo; koma Iye! Aleluya!

210 Mbewu yachifumu idzawawona Iwo. Kodi inu simukumuwona Malaki 4 akufika pokwaniritsidwa? “Kubwezera kubwerera ku Chikhulupiriro chapachiyambi, Mawu a Mulungu!” Ndithudi anthu inu mukhoza kuwona zimenezo. Ife sitikuyenera kuti tizipange izo momveka bwino. Musiye chipembedzo chimenecho chizipita. Munthu, bwererani ku Mawu amenewo. Ndipo Liwu la tsiku lotsiriza, ndi chizindikiro cha tsiku lotsiriza, ndi zoti zidzawatembenezire anthu kubwerera ku Chikhulupiriro chapachiyambi, Malaki 4 ananena chomwecho, kubwerera ku Mawu.

211 Ndipo Iye anali Mawu, osati mkazi; Iye, ameni, Dzina la Ambuye Yesu; Mawu otsimikiziridwa tsopano mwa lonjezo, Mawu amene analonjeza.

212 Yohane Woyera 14:12, “Ntchito zimene Ine ndizichita, inunso mudzazichita.” Malaki 4, chinthu chomwecho chimene chinanenedwa pamenepo. Ndiponso, Luka 17 amatiuza ife, kuti, mmasiku otsiriza mawonetseredwe a dziko adzakhazikitsidwa ndendende basi mu dongosolo, “monga izo zinali mmasiku a Sodomu,” ndipo Mulungu akanadzabwera pansu, nkudzawonetseredwa mu thupi la munthu, ndipo nkumadzadziwa zinsinsi za mmitima. Hmm, hmm. Yesu ananena chinthu chimenecho, ndipo icho chikanadzachitika, “mmasiku amene Mwana wa munthu akuwululidwa,” ku mapeto a dziko lapansi.

Mwaona, si mpingo, “Kujowina *ichi*, kujowina *icho*.”

213 Ndizo, kubwera kwa Iye! Ndicho chimene mbewu ya Abrahamu inapeza kumeneko, nsembe yoperekedwa, mmalo mwa mbewu yake yeniyeni. Nanga bwanji Mbewu yake yauzimu, ameni, Mbewu Yake yachifumu, Mbewu ya Mfumukazi? Ameni.

Oh, ngati inu mukanangochiwona icho! Kumbukirani, ndi chiyani chimenecho? Ndi thupi ndi Mzimu kulumikizana, kudzakhala chimodzi.

²¹⁴ Taonani mu Mateyu, mutu wa 3. Apa panali thupi, Mwana wa Mulungu wobadwa mwa namwali, akubwera pansu kuchokera mu—mu mzindawo, anatulukira kupita kwa Yohane M'batizi.

²¹⁵ Ndipo ndi uyo pamenepo, atayima mmadzi. Baibulo linati, “Mawu a Ambuye nthawizonse amadza kwa mneneri.” Ndi kulondola uko? Ndipo Yohane anali mneneri. Iwo anali alibe mneneri mu zaka handiredi.

²¹⁶ Koma apa iye anali, mneneri atayima pamenepo, ndipo iye anali akunenera kuti Yesu akanadzabwera. Iye anali ali uko mu chipululu, ndipo anati iye anawona chizindikiro. Mulungu anamuuza iye kuti chizindikiro chimenecho chikanadzamutsatira Mesiya ameneyo, pamene Iye adzabwera. Iye anati, “Iye wayima pakati panu penapake tsopano. Alipo Mmodzi pakati panu, Yemwe nsapato zake ine sindiri woyenera kumasula. Iye adzawonetseredwa limodzi la masiku awa. Ndipo pamene Iye adzatero, ndiye ine ndidzachepe, Iye adzakwera.”

²¹⁷ Iye anapezeka kuti ayang'ane, ndipo anawona chizindikiro chimenecho; iye anati, “Apa Iye akubwera tsopano. Taonani Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo lake la dziko lapansi.”

²¹⁸ Mlaliki wakale wa Baptisti, Dokotala Davis, yemwe anandibatiza ine mu chiyanjano cha mpingo wa Baptisti, anakambirana izo ndi ine nthawi ina. Iye anati, “Iwe ukudziwa chimene chinachitika kumeneko, Billy?”

Ndipo ine ndinati, “Ayi, ine sindikutero, Dokotala.”

²¹⁹ Iye anati, “Apa ndi zomwe zinachitika. Yohane anali asanabatizidwepo.” Anati, “Yohane anamubatiza Yesu, ndipo kenako Yesu anatembenuka ndipo anamubatiza Yohane.”

Ine ndinati, “Ine—ine sindikudziwa za zimenezo.”

²²⁰ Chotero ine ndinapitiriza kupempherera za izo. Usiku wina mmasomphenya, apa pali chimene icho chinali. Mukuona? Iye sanatero, Iye sanabatize konse, Yesu sanamubatize konse Yohane. Chabwino, chiyani?

²²¹ Iye anati, “Ine ndiyenera kubatizidwa ndi Inu, ndipo chifukwa chiyani Inu mukubwera kwa ine?”

Yesu anati, “Balola kuti izo zikhale chomwecho.”

²²² Penyani maso awiri amenewo, amuna awiri aakulu pa dziko lapansi; *apo* panali Mulungu, *apa* panali mneneri Wake, ndipo Mawu amadza kwa mneneri. Ngati Mawu ali mu thupi, Iwo adzapita kwa mneneri. Ziribe kanthu kumene Iwo ali, Iwo adzapita kwa mneneri. Iwo ayenera kutero. Baibulo linanena

chomwecho. Ayi . . . Ndipo apa pakubwera . . . Iye anali Mawu. “Pachiyambi panali Mawu. Ndipo Mawu anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Ndipo apa pakubwera Mawu kwa mneneri, kumeneko mmadzi momwe, kuti akakwaniritse ndi kutsimikizira uneneri wake. Amen. Apa Iye wayima pamenepo, ndipo apa maso awiri amenewo akukomana wina ndi mzake; mmodzi mneneri, ndipo mmodzi winayo Mawu.

²²³ Ndipo iye, Yohane, wodzichepetsa pamaso pa Iye, iye anati, “Ine ndiyenera kubatizidwa ndi Inu, ndipo chifukwa chiyani Inu mukubwera kwa ine?”

²²⁴ Iye anati, “Balolani kuti zikhale chomwecho, pakuti zikuyenera kwa ife,” chikutikakamiza ife, mwaona, “zikutiyenera kukwaniritisa chirungamo chonse.”

²²⁵ Yohane, pokhala mneneri ndipo ankawadziwa Mawu amenewo, chifukwa Mawu anabwera kwa iye, iye ankadziwa kuti imeneyo inali Nsembe. Ndipo molingana ndi Chilamulo, Nsembe inkayenera kuti itsukidwe isanaperekedwe. Ndizo ndendende. Iye anamubatiza Yesu chifukwa Iye anali Nsembe yakudza. Iye asanapite ku moyo Wake wapagulu, Iye ankayenera kuti abatizidwe, chifukwa Nsembe iyenera kutsukidwa isanaperekedwe. Amen. Ndipo iye anamubatiza Iye.

²²⁶ Ndipo pamene iye anatero, Iye anapita molunjika kutuluka mmadzi. Ndipo anayang’ana mmwamba ndipo anawona Mzimu wa Mulungu, ngati nkhunda, ndi Liwu likuchokera kwa Iwo, linati, “Uyu ndiye Mwana Wanga wokonedwa mwa Yemwe ine ndikukondwera kukhalamo.” Mulungu ndi munthu anadzakhala mmodzi.

²²⁷ Adamu ndi Eva anali mmodzi, pachiyambi. Ndipo pamene Iye anawalekanitsa iwo, iye anagwa, chifukwa cha Mawu. Iye anaphonya Mawu. Iye anagwa.

²²⁸ Chomwechonso m’badwo wa mpingo uliwonse wagwa monga chomwecho, pa chifukwa cha kutanthauzira molakwika Mawu. Kulola wotanthauzira, Satana uja kuti awatanthauzire Iwo kwa Eva, “Oh, ndithudi *Izo* sizikanakhoza kukhala zoon. Ndithudi *Izi*, ndithudi *izi* zonse sizingakhoze kukhala. *Izi* sizingathe. Oh, inde, ine ndikudziwa, ndithudi . . .”

²²⁹ Koma ngati Mulungu ananena chomwecho, izo zikupanga Iwo chomwecho. Palibepo ayi “ndithudi” kwa Iwo. Inu muyenera kubadwa mwatsopano. Inu muyenera kulandira Mzimu Woyera. Kapena zimenezo kapena kuwonongeka! Zindikirani.

²³⁰ Ndipo apa Iye—apa Iye anabwera mmenemo, Yesu ndi Mulungu anakhala mmodzi. Iwo analumikizana.

²³¹ Monga mu Edeni, kumene kumeneko Adamu ndi Eva anali pachiyambi, mzimu womwewo. Mayina awo ankatchedwa Adamu. Mukuona? Iye anali ziwiri zonse Adamu ndi Eva,

limodzi. Ndipo pamene analekanitsidwa, kuti ayesedwe, chinachitika ndi chiyani? Eva anagwa, ndi Mawu. Amenewo anali Mawu. Adamu anamutsatira iye, kuti akamuwombole iye, koma iye sanakhoze kuchita zimenezo. Iye sanali woyenera kumuwombola iye.

²³² Ndiye kenako panadzabwera Adamu Wachiwiri, kuti adzawuwombole Mpingo, umene unali mu mthunzi ndi choimira.

²³³ Tsopano, motsimikiza basi monga Adamu ndi Eva ankayenera kukhala mzimu womwewo, Khristu ndi Mpingo ayenera kukhala Mzimu womwewo, utumiki womwewo. “Zinthu zimene Ine ndizichita inunso muzidzazichita.” Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Izo ankayenera kuti agwirizane pamodzi. Thupi ndi magazi, ndi Mulungu, zinkayenera kubwera pamodzi ndi kukhala Mzimu umodzi. Ndipo Yesu Khristu ndi Mpingo Wake ndiwo Mzimu umodzi. Mpingo ungakane bwanji chirengedwe, mpingo ungakane bwanji chinthu chimene Khristu anawauza iwo kuti adzachte, ife tingawukane bwanji Iwo ndiyeno nkudzanena kuti ndife a Khristu? “Ngati inu mukhala mwa Ine, ndi Mawu Anga akakhala mwa inu, pemphani chimene inu muchifuna, ndipo icho chidzapatsidwa kwa inu. Ine ndine Mpesa, inu ndinu nthambi, ndipo Moyo umene uli mu mpesa umapita mu nthambi kukabala chipatso.” Obala-zipatso!

²³⁴ “Ndipo nthambi iliyonse yomwe siyibala zipatso zabwino, imadulidwapo.” Umo ndi momwe mabungwe ankachitira, kuziswa izo, kuwasakaniza Mawu, ndi kuyamba monga chomwecho. Ndipo wina akuyamba njira *iyi*, ndipo wina njira *iyi*, ndipo, chinthu choyambirira inu mukudziwa, kagulu kakang’ono kochepa ka ma Ricky kamabwera umo ndipo iwo amapeza lingaliro lawo mu zimenezo, ndipo, chinthu choyambirira inu mukudziwa, ndiye ilo langokhala gulu lalikulu la Babeloni. Iye amangozidulapo izo.

²³⁵ Palibe bungwe linayamba lawukapo, koma chimene ilo linagwa. Ndipo mmodzi aliyense amene anagwa, sanadzabwererense konse kachiwiri. Ine ndikutsutsa zimenezo kwa aliyense. Inde, bwana. Inu mukuidziwa mbiriyakale. Sipanakhalepo mmodzi. Mulungu, mwamsanga pamene iwo apanga bungwe, Iye amawaika iwo pa alumali, ndipo izo zimathetsa izo. Iye adzatenga munthu kuchokera kwinakwake, kuzibweretsa izo pomwepo. Ndithudi.

²³⁶ Zindikirani mu izi tsopano, iwo ayenera kukhala mmodzi. Yesu anati, ndiye, “Moyo umene uli mwa Iye udzakhala mu Mpingo Wake.” Ndipo apa pali ndendende zimene Iye analonjeza mmasiku otsiriza, kuti Moyo umene unali mwa Khristu, umene unali mwa . . . udzawonetseredwa mmasiku amene dziko lidzakhale mu chikhalidwe cha Sodomu chimodzimidzi monga

momwe izo ziliri tsopano. Kodi inu simukuwona, m'bale, mlongo?

237 Zikuchita ubwino wANJI kulowa mpingo ngati mulibe Khristu mmoyo wanu, ndi Khristu kudzizindikiritisa Yekha mmoyo wanu? Mwaona, ndi zimenezotu. "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Iye ananena zimenezo. Kodi inu munganene bwanji izo, ngati izo si choncho, inu mungadzinere bwanji kuti ndinu a Khristu?

238 Inu mukuti, "M'bale Branham, kodi inu mukuganiza kuti mupanga bwanji izo kuti zimamatirane ndi anthu, mu tsiku laluntha ili pamene chirichonse chiri chipembedzo?"

239 Ine ndinamufunsa mkazi, osati kale kwambiri, "Kodi ndinu Mkhristu?" Mu chipatala. Iye anati, "Ine ndikupatsani inu kuti mumvetsetse kuti ine ndimayatsa kandulo usiku uliwonse." Ngati kuti izo zinali ndi chirichonse chochita ndi Chikhristu? Ine ndinali. . .

240 Ine ndinapita kukapempherera mkazi wina, ndipo ine. . . dona wina anali atagona pamenepo, akudwala, iye ndi mwana wake wamwamuna. Ndipo ine ndinati. . . Ine ndinalowa mkati. Ine ndinati, "Dona, kodi inu mutero. . . Eya," Ine ndinati, "Ine ndikudziwa yemwe inu muli. Ndinu Akazi a Oliver."

241 Iye anati, "Inde, M'bale Branham." Iye anati, "Ine ndakhala ndikudwala kwambiri, M'bale Branham. Adokotala sakukhoza kupeza chimene chiri cholakwika ndi ine. Kodi inu mungapereke pemphero? Ndicho chifukwa ine ndinakuitanani inu."

242 Ine ndinati, "Ndithudi, Mlongo Oliver." Ine ndinati, "Kodi mungadandaule kuweramitsa mutu wanu?"

243 Anati, "Dikirani miniti yokha! Kokani katani imeneyo!"

244 Ndipo ine ndinati, "Chabwino, chabwino." Ine ndinati, "Ine ndingopemphera. Kodi ndinu Mkhristu?"

Iye anati, "Ndife Amethodisti."

245 "Chabwino," Ine ndinati, "zimenezo si zomwe ine ndinakufunsani inu. Ine ndinakufunsani ngati inu muli Mkhristu."

Iye anati, "Kokani katani imeneyo!"

246 Mwaona, ndiko basi kuwonda kwake. Kodi zingatheke bwanji munthu kukhala? Ndiko kuda ndi mdima, kusiyana kwa zipembedzo kuwachotsa iwo ku madalitso a Mulungu. Zimenezo zimakhala mu zipembedzo zonse. Ndiko kulondola. M'bale, musapite kwa *mkaziyo*; pitani kwa Iye. Musatenge dzina la *mkaziyo*; mutenge Lake, mwaona, mutenge Dzina Lake.

247 Inu mukuti, "M'bale Branham, inu mupanga bwanji izo kuti zimamatire lero? Inu muzichita motani izo?"

248 Iye anapanga lonjezo kuti Iye akanadzatero, anati, “Musawope, kagulu ka nkhosa, ndicho chifuniro chabwino cha Atate anu kuti akupatseni inu Ufumu.”

“Kodi Iye achita motani zimenezo?”

249 Iye akadali Yehova-Yire. Iye akadali Yehova-Yire. Mulungu akhoza kudzipezera Yekha Mpingo. “Iye ndi wokhoza mwa miyala iyi kuwutsira ana kwa Abraham.” Iye, ndithudi, Iye ndi Yehova-Yire.

Inu mukuti, “Kodi izo zidzagwira ntchito?” Ndizo zoonā. Mulungu analonjeza izo.

“Kodi inu mukuganiza kuti inu mudzakwanitsa konse zimenezo . . .?”

250 Ine sindingakhoze, koma Iye angatero. Ine ndiribe udindo wowapangitsa Iwo kuchita zimenezo. Ine ndiri nawo udindo wolalikira Iwo. Ndi ntchito Yake kuti awatsimikizire Iwo. Ndi Iyeyo. Ngati ine ndiyima ndi Choonadi, Iye adzayima nacho Icho. Iye wazitsimikizira izo, ndipo Iye adzachita zimenezo.

Inu mukuti, “Ndi mdima wowopsya.”

251 Inde, ine ndikudziwa kuti ndi mdima wowopsya. Ndipo azibusa onse akupita mu bungwe lalikulu kwambiri ili, kuti akaphedwe.

“Kotero inu muchita chiyani za zimenezo?”

252 Zimangondikumbutsa ine za kankhani kakang’ono. Ine ndikhoza kunena izi ndisanatseke. Uko mu Carlsbad, New Mexico, kuno, iwo ali ndi mapanga uko, inu mukudziwa. Iwo—iwo amayenera kuti atsikire pansi pafupifupi mailosi, pansi mmenemo. Ine sindinayambe ndazikondapo zinthu zimenezo. Nthawi zonse zimakhala ngati mole mu nthaka. Ndipo iwo unapita pansi mmenemo, ndipo, oh, kumakhala mdima pakati pa usiku pansi kumeneko. Ndipo pali mtsikana wamng’ono uyu waimirira, oh, mwinamwake, monga kanthu kakang’ono ako *pamenepo*. Ndipo mchimwene wake wamng’ono anali atayima cha *apa*, kumbali imodzi, ali ndi namulondola yemwe anali kuwatengera iwo pansi. Kotero iwo anali atayima pansi mu malo a mdima awa, ndipo apo panali kuwala pamenepo, anali atayatsa nyali zonse. Ndipo bambo uyu, basi kwa . . .

253 Namulondolayo anazembera ku kuwalako. Ndipo mnyamata wamng’ono uyu anali kuyenda naye iye, akumuyang’anitsitsa namulondolayo. Kotero namulondola anafika kumeneko, ndipo anatenga switchi iyi ndipo iye anangokhethemula kuizimitsa switchiyoy. Oh, mai, kuyankhula za mdima! Mailosi kuya kwake pansi, inu mukudziwa, mdima kwambiri iwe sungakhoze kugwedeza dzanja lako, sungakhoze kuwona kalikonse.

254 Ndipo mtsikana wamng’ono ameneyo anali kukuwa ndi zonse zomwe zinali mwa iye. Iye anali akungolumphā chokwera-ndi-chotsika ndi kumakuwa, kukuwa mwamphamvu momwe . . .

255 Ndipo kukuwa konseko, mnyamata wamng'onoyo ataimirira kumbali imodzi, iye anati, "Oh, mlongo wamng'ono! Oh, mlongo wamng'ono!"

Iye anati, "Kodi iwe ukufuna chiyani, m'bale wamng'ono?"

256 Anati, "Musachite mantha. Pali mwamuna pano amene akhoza kuyatsa kuwala."

257 Pali Mwamuna pano amene akhoza kuyatsa Kuwala. Iye, Iye ndi Yehova-Yire. Mukuona? Pali Mwamuna pano, amene ali pakati pathu usikuuno, Mzimu Woyera, Iye akhoza kuyatsa Kuwala. Iye ndi Mawu, Mwamuna pano amene akhoza kuyatsa Kuwala. Ine sindikudziwa momwe Iye ati achitire izo. Si za ine kuti ndidziwe, koma Iye amadziwa momwe angayatsire. Iye anapanga lonjezo. Iye anazipanga izo apo pamene Abraham anali ndi mpeni wake pamwamba pa khosi la mwana wake; Iye anayatsa Kuwala. Eya. Iye akhoza kuyatsa Kuwala kachiwiri usikuuno.

258 Tiyeni tiweramitse mitu yathu miniti yokha. Mulungu atithandize, kuti Iye ayatse switchi yaing'ono imeneyo mu mtima mwanu.

259 Abwenzi, sabata ino inu mwawona Mzimu Woyera waukulu pakati pathu. Palibe funso kwa izo. Koma, oh, mulole Kuwala kwakung'ono uko kuyatsidwe, usikuuno. Musati mukuphonye Iko, m'bale wanga, mlongo. Ine ndikuganiza izo basi ndi mutu wawung'ono uwu apa wa—wa Abraham, zatsimikizira, basi kungozilumikiza izo mmbuyo ndi mtsogolo, kuyambira ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso, zatsimikizira ora lomwe ife tikukhalamo; Khristu, wakanidwa mu fuko lathu kachiwiri; zivomezi mmalo osiyanasiyana; Sodomu ndi Gomora; mpingo mu chikhalidwe chake, ndendende kupanga fano la chirombo. Zinthu zonsezi zachitika, monga Baibulo linanena, ndipo anthu inu mukudziwa zimenezo. Mukuona? Tsopano popanda chokuchitikirani chachikulu ichi ndi Khristu, ngati Moyo wa Khristu ubwera mwa inu. . .

260 Tsopano mungodziyang'ana nokha mu kalilole wa Mulungu, ndipo mungowona ngati inu mungathe kudzizindikiritsa nokha usikuuno. Ngati inu mukanakhala mukukhala mmasiku a— a Nowa, mu nthawi ya chigumula, ndi mbali iti yomwe inu mukanazindikirika nayo? Ngati mukanakhala mmasiku a Mose, kodi inu mukanakhala muli mbali iti? Ngati mukanakhala moyo mmasiku a Khristu, pamene mipingo yonse inali kumutsutsa Iye? Iye ankayenera kuti ayime yekha kunja uko, ndi zinthu zimene Iye ankazichita. Chinthu chokha, chinali Mulungu ndi Iye, ndicho chinthu chokhacho. Ngakhale ophunzira Ake onse, pafupifupi, anamuchokera Iye. Koma mbali iti, basi khalidwe lanu la pano, inu mungakhale kuti, inu mudzakhala mbali iti? Ndi mbali iti yomwe inu mungakhale muli pakali pano, pamene inu mudzamuwona Iye kachiwiri pakati pathu pomwe?

261 Tsopano Iye ali pano, ndipo akhoza kuyatsa Kuwala mu mtima mwanu, ndi kungowudzaza moyo wanu ndi Mzimu Woyera. Ndi angati muno tsopano, ndi mitu yanu yoweramitsidwa, ndi mitima yanu, nanunso, mungapemphere ndi ine mphindi yokha?

262 Tsopano, Atate Akumwamba, ife tikudziwa kuti Inu basi simumangobwera pamenepo ndi—ndi kudzachita zinthu kusonyeza kuti Inu mukhoza kuchita izo. Inu mukuchita izo kwa cholinga. Ndipo, Ambuye, sabata ino, ine ndinamverera kutsogozedwa kuti ndidikire mpaka miniti iyi, nthawi yomweyi, kuti choyamba iwo adzawona kuti Mawu akutsimikiziridwa. Ndi zoposa funso lirilonse tsopano. Ndipo khalidwe limodzi ili, Abraham, pamene makhalidwe onse mu Baibulo amangirizidwa kumene mwa ilo, ndipo ife tikuwona pamene ife takhala pakali pano.

263 Atate, ndi mawu osweka, koma ndicho chopambana chimene ine ndikanakhoza kuchita. Ine ndikupemphera tsopano kuti Mzimu Woyera wawukulu umene uli pano, umene umadziwa chinsinsi cha mtima uliwonse, uyankhule ndi mtima umenewo pakali pano. Chitani, Ambuye. Yankhulani kwa uyo amene sakanati apite, ngati Inu mukanabwera usikuuno, ngati chitseko chikanatsekedwa usikuuno, ngati iwo akanafera panjira popita kwawo, kapena kugundidwa ndi galimoto ndi kufa, kapena kufa, kupezeka atafa pa bedi mmawa, iwo sakanakhoza kupulumutsidwa. O Mulungu, chonde musalole aliyense wa iwo apite mwanjira imeneyo.

264 Ngati iwo angojowina kumene mpingo, Ambuye, mulole iwo asachite manyazi kuti atuluke ndi kudzamupempha Mulungu kuti awadzaze Mzimu Wake, kuti Moyo Wake ubwere mwa iwo. Ngati iwo sanakhoze kumvetsa zinthu izi; ngakhalenso akuphuzira aja, koma iwo anagwiritsitsabe kufikira Mzimu Woyera unatsanuliridwa, ndiye iwo anamvetsa Izo, ndipo analemba Baibulo. Ine ndikupemphera, Atate, tsopano, kuti Inu muyankhule kwa mtima uliwonse ndipo mulole iwo adziwe kuti Mwamuna amene akhoza kuyatsa Kuwala ali pakhomo pomwe pa mtima wawo.

265 Ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano. Ndi angati muno ati akhale owonamtima kwenikweni, ndi kuti, “M’bale Branham, ine—ine ndikudziwa kuti ine sindiri paubale ndi Mulungu”? Ine ndikufuna—ine ndikufuna inu kuti mukweze dzanja lanu mmwamba. Ingoweramitsani mutu wanu, aliyense, koma kwezani dzanja lanu. “Ine sindiri paubale ndi Mulungu.” Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Inde. “Ine,” manja, “Ine ndikudziwa ine sindiri paubale ndi Mulungu.”

266 Mukuona, chimene ine ndikuyesetsa kuti ndichite, kupeza kukonderedwa ndi Mulungu chifukwa cha msonkhano wawukulu wamachiritso uwu mawa. Ngati nditangokhoza

kupeza kukondoledwa, ine—ine—ine sindikukhulupirira kuti pakhala chinthu chiti chidzasiyidwe, koma chimene chiti, Mulungu achiza, ngati ine ndingakhoze kuwapangitsa anthu kuti akhulupirire.

²⁶⁷ Tsopano, inu opanda ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo inu mukudziwa kuti amenewo ndi Mafuta. Ngati inu munalibe Mafuta mu nyali, iwo sanalowe mmenemo.

²⁶⁸ Ndipo kodi inu munayamba mwamvapo za nthawi yoteroyo, mu mapepala, kumene Apresbateria, Achilutera... Yang'anani pa magazini ya Amuna Amalonda Achikhristu. Achilutera, Apresbateria, ngakhale Akatolika, akufunafuna kuti aupeze ubatizo wa Mzimu Woyera, mwa mazana. Ndipo ine ndikudabwa ngati Amuna Amalonda a Full Gospel awo akumvetsa kuti iwo sadzaupeza Iwo?

²⁶⁹ Baibulo linati, “Pamene iwo anabwera, anati, “Tipatseniko ena a mafuta anu, iwo anatero.” Namwali wogona, iwo anazindikira kuti iwo anali nayo nthawi yonseyo kuti atenge Mafuta, koma iwo sanachite zimenezo. Chotero pamene Mkwati anali pafupi kubwera, iwo anati, “Tipatseniko ena a Mafuta anu.” Iwo anati, “Ife tangotsala nawo otikwanira ifeeni. Inu pitani mukagule kwa iwo amene akugulitsa.” Ndipo pamene iwo anali atapita, Mkwati anabwera, ndipo Mkwatibwi analowa mkati. Ndipo iwo anaponyedwa ku mdima wakunja, kuti akawuke ndi kudzapeza kuti Mkwatulo unali utapita. “Ndipo iwo anasiyidwa kumene kudzakhala kulira ndi kubuma,” nthawi ya Chisautso, “ndi kukukuta kwa mano.”

²⁷⁰ M'bale wanga, mlongo, usikuuno, mzanga, ngati inu mulibe Mzimu Woyera, kodi inu... kapena mwatsutsidwa mokwanira kuti mwadziwa kuti inu muyenera kukhala nawo Iwo, kodi inu mungakweze mmwamba dzanja lanu, mukuti, “Ndipempherereni ine, M'bale Branham. Ine ndikukhulupirira ife tiri mu Kukhalapo kwa Mulungu. Ndipempherereni ine. Ine ndiribe Mzimu Woyera.” Mulungu akudalitseni inu. Tangoyang'anani pa manjawa, paliponse. Kodi inu mukuwufuna Iwo, ndiye?

²⁷¹ Tsopano ine ndikudziwa, kwa inu Amethodisti ndi Abaptisti, ndi ena otero, pamakhala kutengeka kochuluka kumene kumatsatira uthenga uliwonse.

²⁷² Tsopano kwa inu Achilutera. Ine ndinali kungowerenga mbiriyakale ya Martin Luther, limodzi la mabuku ake linalembedwa pa iye, kuno osati kale kwambiri. Iwo anati, “Izo sizinali zachinsinsi kwambiri kuti Martin Luther akanakhoza kutsutsa mpingo wa Katolika ndi kupitirira nawo iwo, koma kugwira mutu wake pamwamba pa zotentheka zonse zomwe zinatsatira chitsitsimutso chake.”

²⁷³ Ndipo izo zimachitika, pamakhala unyinjira wosakanizika ndi chitsitsimutso chirichonse. Inu mukudziwa zimenezo. Koma

tsopano, kumbukirani, izo zimangosonyezera kuti amakhalapo weniweni. Pamene inu muwona dola yabodza, kapena winawake akupanga ngati ali ndi chinachake, ingokumbukirani kuti ilipo imodzi yeniyeni yomwe inapangidwa kuchokerako. Ngati si choncho, ndiyo yapachiyambiyo. Mukuona? Kotero inu mudziwa kuti iyo siyingakhale yapachiyambiyo, kotero payenera kukhala yapachiyambi.

²⁷⁴ Ndipo yapachiyambi imeneyo ndi Yesu Khristu weniweni, Mmodzi yemwe ali pano, yemwe akudziwa chinsinsi chirichonse mu mtima mwanu pakali pano. Ndipo tsopano ine ndikufunsani inu, ngati inu munamuwona Iye, ndi kumva maumboni awa a mitundu yonse ya zinthu akuchiritsidwa, ndi momwe mitima ya anthu yadziwidwira kudutsa mu sabata ino, ndi inu . . . Ameneyo ndi Iye akuyankhula kwa inu. Ndi Iyeyo. Ine ndikudabwa ngati inu mungakhulupirire kuti ine kupemphera, ndi chifukwa cha inu, zingakuthandizeni inu?

²⁷⁵ Kumbukirani, Mzimu Woyera unaperekedwa mwa kusanjika kwa manja. Petro, Filipino atatha kupita ku Samariya ndi kuwabatiza anthu onse kumusi kumeneko, mu Dzina la Yesu Khristu, komabe, Petro anatsikirako ndipo anadzaika manja pa iwo, ndipo Mzimu Woyera unadza pa iwo. Mukuona?

²⁷⁶ Tsopano ngati inu mukukhulupirira mu zimenezo, ine ndikudabwa ngati inu mungabwere kuno, mmodzi aliyense amene sanapulumsidwe, kapena alibe Mzimu Woyera, abwera pano ndi kudzayima pomwe pano miniti yokha, kundirola ine ndikupempherereni inu. Ngati inu mutangobwera kuchokera mkanjira, ziribe kanthu komwe inu muli, mudzangoima pano. Ingoyendani wa kuno ndi kundirola ine—kundirola ine ndipemphere nanu mphindi yokha. Mulungu akudalitseni inu.

²⁷⁷ Tsopano basi aliyense ayimbe tsopano. *Pafupifupi Kukopedwa*, ngati inu mungathe. Mlongo Downing, pano, ngati inu mungatero. Chabwino.

²⁷⁸ Kodi inu simubwera motsatira *apa*, abale anga? Mulungu akudalitseni inu, m'bale wanga. Aliyense ali chete kwenikweni tsopano, akupemphera. Iyi ikhoza kukhala mphindi yofunikira, ikhoza kutanthauza kusiyana pakati pa imfa ndi Moyo, kwa ambiri, anthu ambiri.

²⁷⁹ Inu nonse mwakhala muli kuno sabata ino? Kodi inu mwawuwona Mzimu Woyera, zomwe Iwo wachita sabata ino pakati pa anthu?

“ . . . -ded,” Khristu kuti alandire;

Oh, Iye ali tsopano, solo ina kuti . . .

²⁸⁰ Kodi inu simungabwere, opanda Mulungu, opanda Mzimu Woyera? Kodi inu mukuti, “Ine ndine wa mpingo, M'bale Branham”? Ndizo zomwe, si zomwe ine ndikuzikamba. Ine ndikutanthauza, kodi inu mwadzazidwa ndi Mzimu wa Mulungu?

“...zochuluka...”

281 Inu simudzapeza konse tsiku loyenera kwambiri kuposa pakali pano, pamene Yesu Khristu wazindikiritsidwa pakati pathu.

“...pa Inu...”

282 Bwanji ngati inu mutafa mmawa usanafike? Ndiyeno inu simungakhoze kuyitana. Kodi inu simubwera tsopano pamene Iye akuitana?

“Pafupifupi kukopeka,”...

Uko nkulondola, zibweranibe kumatsikira kuno.

...bwerani, bwerani lero;

“Pafupifupi kukopedwa,” osatembenuka...

283 Kodi inu simubwera tsopano? Ine ndikudziwa chinachake mu mtima mwanga chikundiiza ine kuti pali winawake akudziletsa. Musachite zimenezo, m'bale, musachite zimenezo!

...Angelo akuyandikira pafupi,

Mapemphero akuwuka kuchokera mmitima
mokonedwa; Woyendayenda, bwera.
(Tsopano kwenikweni...)

284 Mvetserani, mzanga. Inu mukukhulupirira kuti Mzimu Woyera, kudutsa sabata ino, watsimikizira kuti Iye akuyankhula pano? Tiyeni tiwone dzanja lanu. Payenera kukhala awa ambiri, kapena ochuluka. Ine ndikumverera Kumverera kumeneko. Mwaona, Iye siali...Pali chinachake cholakwika apobe. Kulibwino mubwere.

285 Kumbukirani, ine sindingakhoze—ine sindingakhoze kukukakamizani inu kuti mubwere motsutsana ndi chifuniro chanu. Koma ine ndikukhulupirira kuti iyi ikhoza kukhala nthawi yake, zonse zomwe inu mukuyembekezera, mwina zikukonzekera kuti zichitike pakali pano. Ndipo izi zikhoza kukhala, ine ndikuyembekeza kuti sichoncho, ikhoza kukhala nthawi yomaliza kuti inu muitanidwe. Kumbukirani, Iye sadzamenyera nthawizonse. Iye adzayitana, ndiye Iye adzatembenuka kuchoka kwa inu, osabwereranso konse.

286 Bwanji inu osabwera pakali pano? Kodi inu simubwera kuno ndi kudzangoziyimira nokha pamaso pa Mulungu? Kudzati, “Ine ndibwera ndidzayime. Ine ndidzatenga njirayo. Ine sindikuchita manyazi. Ine ndi wa mpingo, koma ine ndikufuna kuti dziko lonse lapansi lidziwe kuti ndine wokonzeka kulandira Khristu mu mtima mwanga, Mzimu Woyera. Ine ndikubwera tsopano kuti ndichite zimenezo. Ine ndakonzeka kuti ndiwongoledwe, ndikhale Mkhristu weniweni, dona weniweni, mwamuna weniweni.” Kodi inu simubwera? Iye tingodikirira. Kazibweranibe kuno, ndiko kulondola, kuchokera

mmakonde ndi mkanjira. Kazibwerani kuno, mudzangopanga kuima kwanu.

²⁸⁷ Mzanga, ine mwina sindidzakuwonaninso inu mbali iyi ya nthawi yopambana. Koma ngati ine sinditero, kumbukirani, ine ndidzakhala wosalakwa tsopano, chomwechonso Khristu. Iye wadzizindikiritisa Yekha ndi inu. Inu mudzamuwona Iye akuchita chinthu chomwecho mu kanthawi kochepe. Chabwino. Tsopano bwerani kuno, dzatengeni maimidwe anu.

²⁸⁸ “Bwanji,” inu mukuti, “M’bale Branham, inu mukundiweruza ine.” Ayi, ine sindikutero.

²⁸⁹ Ine ndikuweruza Kumverera uku komwe kuli mwa ine, mwaona. Pali Chinachake mkati muno, chikuti, “Oh, alipo enanso. Palinso ena ochuluka.” Mukuona?

²⁹⁰ Tsopano inu mukuti, “Chabwino, ine, ine ndajowina tchalitchi, M’bale Branham. Ndine wa Chipentekoste. Ine—ine—ine sindikutero. . .” Ine sindikunena zimenezo, mzanga. Ine sindikufunsa zimenezo, nkomwe.

Ine ndikufunsa, “Kodi inu muli nawo Moyo wa Khristu?”

²⁹¹ Ndipo inu mukuti, “M’bale Branham, ine ndinayankhula mmalirime.” Zimenezo ndi zabwino. Koma zimenezo sindizo panobe zomwe ine ndikufunsa.

²⁹² Inu mukuti, “M’bale Branham, ine sindinapwetekepo aliyense.” Zimenezo sindizo apobe zomwe ine ndikufunsa.

“Kodi Moyo wa Khristu uli mwa inu?”

²⁹³ Usazitenge mopepusa, mzanga. Usatero, usatero, usachite zimenezo. Izo zidzakhala pamene iwe. . . Pamene imfa idzakukantha iwe, idzakhala nthawi itatha pamenepo. Usachite zimenezo. Chonde usatero.

²⁹⁴ Tsopano ife tiri nawo ambiri pano pakali pano, ine ndiyenera ndipereke malo pang’ono kwa enanso. Ine ndiwapempherera awa, ndiyeno kuti ife tidzakhoze kulowa mkati, kudzalowa mchipinda umo kuti tibwere tidzaike manja pa iwo, kulandira Mzimu Woyera. Ndiyeno tiwapempherera awa pakali pano.

Inu muweramitse mitu yanu mphindi yokha.

²⁹⁵ Atate athu Akumwamba, apa pali iwo amene awerama apa, amene ali amuna ndi akazi, iwo ndi anthu Amuyaya. Iwo, iwo ayenera azipita, ife tikudziwa zimenezo. Ndipo tikuwona zivomezi, zimenezo, ndipo dziko mmalo omwe ilo lirimo tsopano. Ndi kumuwona Khristu akubwera kwa ife ndi kumachita zinthu zomwe Iye akuchita, ndi kuwona Uthenga, Mawu akutulukira kumeneko, ndiyeno nkumuwona Iye akubwera kuseri kwa Iwo ndi kudzawatsimikizira Iwo kuti ndi Choonadi, akudziwa chinsinsi chirichonse cha mtima. Ndipo anthu awa tsopano abwera kutsogolo kudzapanga kuima. Iwo sakanakhoza kuchita

izi mwa iwoeni. Iwo abwera chifukwa iwo anatsogozedwa kuti abwere.

²⁹⁶ Ndipo, Atate, ine ndikupereka pemphero kwa iwo pomwe pano. Osati kokha chifukwa cha chipulumutso chawo, kuti apulumutsidwe, koma iwo akhoze kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Perekani izi, Ambuye. Mulole mmodzi aliyense amene wayima pano adzazidwe ndi Mzimu, ndipo mulole kuchokera pano pabwere chitsitsimutso kudutsa dziko lino, chimene chiti chidzagwedeze gulu ili ndi dziko lonse lozungulira. Perekani izi, Ambuye.

²⁹⁷ Ndipo mpingo uliwonse, ndi Methodisti, Baptisti, Presbateria, mpingo wa Khristu, Lutheran, chirichonse chimene chingakhale, mulole mubwere chitsitsimutso, Ambuye, mwa anthu awa akubwerera kwawo ndi Mzimu Woyera weniweni ukuwonetsera Mulungu mmiyoyo yawo. Perekani izi, Atate. Iwo ndi Anu tsopano, ndipo ine ndikuwapereka iwo kwa Inu. Tsopano ife tiwatengera iwo mkati ndi kuika manja pa iwo, Ambuye, kuti iwo akhoze kulandira Mzimu Woyera. Mu Dzina la Yesu.

Tsopano pamene ife tonse tiri ndi mitu yathu pansi.

²⁹⁸ Ine ndikupempha gulu *ili* tsopano, limutsatire bambo *uyu* pomwe apa pambali yanu, kuti iye afike, ife tifikenso kwa inu kuno mchipinda. Ife tiri nawo malo apa oti inu mugwade pansi; ife tibwere tidzaike manja pa inu, kuti inu mulandire Mzimu Woyera. Ndipo ngati inu mukudwala, inu muchiritsidwa. Ndipo basi chirichonse chimene inu mukuchisowa, pitani pomwe pano tsopano. Ife tikhoza kulowa mkati ndi inu. Alipo ambiri omwe ayenera kubwera, koma iwo ali—iwo ali pafupi. . . Palibe malo oti iwo adzayime. Ife tikungofuna kupanga holo iyi pawiri; kulondola, pitani mkati umu, kwa iyi—mbali iyi cha *apa*. Uko nkulondola. Mulungu akudalitseni inu.

²⁹⁹ Tsopano, kwa nonse a inu pano tsopano; pamene iwo akutuluka kunja, bwanji inu musunthire pamwamba pomwe pano tsopano aponso, kwa pemphero. Ndipo ife tidzadzitse malo ano kachiwiri, kuzungulira kuno tsopano.

³⁰⁰ Ife tikupita mmenemo kuti tikalandire ubatizo wa Mzimu Woyera. Ife tikulowa mkati.

³⁰¹ Titatha kuwona kuzindikiritsidwa kwa Ambuye Yesu kuja pano patsogolo pathu, sabata ino, ndi kudziwa kudutsa mthunzi wa kukaikira, kuti ameneyo ndi Iye pano. Tsopano kumbukirani, Mzimu Woyera womwewo, Yesu yemweyo amene akanati andiuze ine chomwe chinali vuto ndi anthu amenewo, kumene iwo anali, amene iwo anali, kumene iwo anachokera, chimene chiti chidzawachitikire iwo. Ndipo inu mukudziwa izo sizinalepherepo nthawi imodzi; ndipo izo sizidzatero konse, sizidzatero konse. Mzimu Woyera womwewo unandiuza ine kuti

ndichite izi. Uko nkulondola. Ine ndikuchita izo mwa utsogoleri wa Mzimu Woyera.

³⁰² Tsopano pamene ichi, mwamsanga pamene gulu ili lituluke mchipinda china ichi apa, ife tisanapite kumeneko, ife tikufuna kuti inu mubwere tsopano. Inu pano, bwerani, sunthirani mmwamba mbali iyi tsopano. Nonse a inu pano amene mukufuna ubatizo wa Mzimu, kodi inu simubwera pakali pano. Yendani chokwera mbali iyi. Mulungu akudalitse iwe, mnyamata. Ndipo ngati ena a inu mukudwala, ndipo simunadzazidwe ndi Mzimu Woyera, bwanji osabwera kudzambulandira Khristu, mumulandire Iye ndiyeno inu muyima bwino usikuuno.

³⁰³ Dona uyu anangokanthidwira pansu ndi . . . iye wakhudzika kwambiri moti iye sakanapirira izo. Iwo akumuthandizira iye kuchipinda. Kazibwerani tsopano, inu, wotsatira wa inu pano tsopano. Pali malo ambiri amene ayima mozungulira tsopano. Kazibwerani kuno, inu amene muli mamembala a mpingo, Amethodisti, Abaptisti. Ife sitikukupemphani inu kuti . . .

³⁰⁴ Mvetserani, abwenzi, ine ndikudziwa iwo akuti, “Pentekoste, iwo anapanga bungwe chipentekoste.” Ndizo zolakwika.

³⁰⁵ Pentekosti ndi chokuchitikira. Amethodisti amachipeza Icho. Abaptisti amachipeza Icho. Onse a iwo amachipeza Icho. Pentekoste si bungwe. Ndi chokuchitikira. Ndipo ngati inu simunakhalepo nacho chokuchitikirani cha pentekoste, bwerani mudzalandire Icho tsopano. Kumbukirani, ngati inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake, mneneri Wake, kumbukirani, ulipo ubatizo weniweni wa Mzimu Woyera. Pakati pomwe pa zotentheka zonse, udakalipobe Mzimu Woyera weniweni, Moyo weniweni. Inu mubwere, mukhulupirire Izo pakali pano.

³⁰⁶ Kodi inu simubwera pamene ife tikuyimba imodzi yokha, ndime zina ziwiri za nyimbo iyi, kuchitira kuti ndikhoze kukhala wotsimikiza kuti moyo wanga wayera pamene ndizichoka mu mzinda uno tsopano, magari sakhala pa iwo? Ine ndikudziwa Iye akuyankhula kwa ena. Bwanji inu osabwera?

“ . . . -ded ” tsopano ku . . . lero;

Mulungu akudalitse iwe, mnyamata wamng’ono. Mulungu akudalitseni inu nonse mwayima pano tsopano.

“Al- . . . ” (Ndiko kulondola. Kazibwerani kuno.) “ . . . - wokopeka kwambiri, ”

³⁰⁷ Bwerani, kuchokera mbali iliyonse ya chipindachi. Kunja, mkati, mmakonde, kulikonseko, kazibwerani mpaka mmusi tsopano, pansu pomwe apa. Dzatengeni malo anu a Khristu. Musachite manyazi ndi Iye. Ngati mukanati mukufa; bwanji ngati inu mukanamva mtima wanu ukudumphapompano?

Ndipo, kumbukirani, Mmodzi uyo amene akuyankhula kwa inu, Iye wagwirizira mtima wanu mdzanja Lake. Iye akudziwa chinsinsi cha mtima wanu. Ine ndikunena izi mu Dzina la Ambuye, alipo ena ambiri pano ati abwere. Bwanji inu simukubwera? Inu mukuti, “Kodi ndi ine, M’bale Branham?” Inde, ndi inuyo. Ngati inu simuli otsimikiza, osati muzengereze ayi.

. . . wokonedwa kwambiri; O woyendayenda, bwera.

“Pafupifupi kukop-. . .” (Ndi zimenezotu. Ndi zimenezotu.) “. . .-ded,” kukolola. . .

Ndiko kulondola, kukolola kwatsala pang’ono kutha. Kazibweranibe.

“Pafupifupi. . .”

³⁰⁸ Tsiku lina, zidzakhala nthawi itatha. Musadikirire ora lina, miniti ina. Dzukani ndipo kazibwerani. Mnyamata, umubweretse bwenzi lako lachikazi. Umubweretse bwenzi lako lachinyamata. Amayi, abweretseni abambo. Kazibwerani, pakali pano, aliyense. Dona wamng’ono, mnyamata, aliyense yemwe inu muli; bambo wachikulire, mayi wachikulire, kazibwerani. Izi ndi zimenezo. Ngati ndinu wokalamba, mukumbukire zimene ine ndakusonyezani inu, pogwiritsa ntchito Baibulo, inu musinthidwa ngati inu muti mungovomereza Mbewu ya Abrahamu.

. . . ndi koma kulephera!
Chisoni, chisoni, kulira kowawa uko:
“Pafupifupi, koma kutayika!”

Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano.

³⁰⁹ Ambuye Yesu, O Mulungu, ufufuzeni mtima uliwonse. Mufufuzeni aliyense, Mzimu Woyera Waukulu. O Mulungu, mulole izo zisakhale pachabe kwa izi, ngakhale munthu mmodzi. Mulole mmodzi aliyense, mmodzi aliyense, Ambuye, apulumutsidwe. Musalole mmodzi wa iwo asochere, Ambuye. Ine ndikuwatenga iwo, mu Dzina la Ambuye Yesu, kwa—chifukwa cha ngale za korona wa Ambuye wanga, oh, Yemwe Kukhalapo kwake kuli pano tsopano, Lawi la Moto lalikulu likuyendayenda kudutsa mchipindachi, likusesa pa mitima. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti mtima umenewo udzadule maunyolo amenewo, ndi kuwuka ndi kubwera mokoma kwa Yesu Khristu, kudzati, “Ambuye, zonse zomwe ndiri, ndiri pano. Nditengeni ine ndipo mundiwumbe ine, Ambuye, mu nyumba Yanu yayikulu yowumbira; ndipo mundidzaze ine, ndi kundipanga ine mwana wamwamuna kapena wamkazi wa Mulungu.” Perekani izi, Ambuye. Mulole izi zikhale chomwecho.

310 Pamene ife tikupitiriza kuyimba ndime ina, mutero inu? Ndiye ife tiyenera kuti titseke tsopano, mwamsanga, chifukwa ife tiyenera kuti tifike kuno ndi ena onsewo.

“Pafupifupi kuko- . . .”

311 Bwerani tsopano. Bwerani pompano, simutero inu? Mulungu akudalitseni inu, wokonedwa. “Mkamwa mwa makanda, Iye amalandira matamando.”

Oh, “Pafupifupi kukopeka,” oh,
musatembenuke nkuchokapo;
Yesu . . .

312 Uyo ndi Iye akukuitanani inu, akuyankhula kwa mtima wanu. “Ndikudabwa ngati ndiri ine?” Ngati pali kachidutswa kamodzi ka kukaikira, bwerani!

. . . akuchedwera pafupi,
Mapemphero amawuka kuchokera mmitima
mokonedwa kwambiri; O woyendayenda,
bwera.

313 Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano, pamene awa akukonzekera. Tsopano pamene inu mwaima apa, ingoyang’anani pansu. Inu mukukumbukira, inu mumabwera mukunena kuti . . . kugunda kwina kwa Chinachake mkati mwanu, kumakuuzani inu kuti pali chinachake cholakwika mmoyo wanu. Ine ndikusirira maimidwe anu. Kumbukirani, Yesu anati, “Ngati mudzachita manyazi ndi Ine pamaso pa anthu, Ine ndidzachita nanu manyazi pamaso pa Atate Anga ndi Angelo oyera. Koma iye amene ati adzandivomereze Ine pamaso pa munthu, iye Ine ndidzamuvo mereza pamaso pa Atate Anga ndi Angelo oyera.”

314 Ndipo tsopano alipo anthu angapo kumbuyo kuno tsopano, omwe ali okonzeka kuti agwirizane nafe tsopano mu pemphero, kuti inu mudzapulumutsidwa ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ingomuuzani Iye kuti inu mukupepesa chifukwa cha zomwe inu mwachita, ndipo inu mukhala Mkhristu kuyambira tsopano, mwa chisomo Chake, ndipo inu mukufuna ubatizo wa Mzimu Woyera umene uti ukutsogolereni inu mu ulendo wa moyo.

315 Atate Akumwamba, iwo ndi ngale kwa korona Wanu. Iwo sakanakhoza kubwera, iwo sakanakhoza kubwera, kupatula Chinachake chitawachenjeza iwo. Ndipo Inu munati, “Palibe munthu angakhoze kubwera kupatula Atate Anga atamukoka. Ndipo onse amene Atate andipatsa Ine adzabwera.” Ndipo apa iwo akubwera, mwa Chinachake chikuwauza iwo kuti abwere. Ndiye Inu mukuiyamba ntchito, Ambuye. Ine ndikupemphera kuti Inu muitsirizitse iyo, usikuuno, mwa iwo, Ambuye, pakuwapanga iwo ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Perekani izi. Mulole mmodzi wa iwo asatayike. Ine ndikuwapereka iwo

kwa Inu tsopano ngati zikho za Mawu Anu ndi Kukhalapo Kwanu. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

³¹⁶ Tsopano bwererani m'chipindamo, mpaka ife tikhoze kufikira kwa inu. Mupite kumanja, apa. Othandizira akutsogolerani inu mukamabwerera.

³¹⁷ Ndipo tsopano—tsopano ine ndikudabwa ngati ogwira ntchito pano angabwere, awatsatira awa mkati, antchito ambiri ochokera ku mipingo ina.

³¹⁸ Inu atumiki amene mukufuna kuti mubwerere mmenemo ndi ife tsopano, kuti mukafufuze ngati izi zachitika molondola kapena ayi, inu bwerani, mubwerere nafe ife. Bwerani, mudzagwade ndi anthu anu, kuti iwo alandire Mzimu Woyera. Mmodzi aliyense, mubwere limodzi ndi . . . Inu atumiki, aliyense wa inu, Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, ziribe kanthu kuti ndinu ndani, kazibwerani. Inu mukuitanidwa. Mubwere ndi anthu awa.

³¹⁹ Ndipo inu antchito othandizira ochokera ku mipingo yosiyanasiyana, amene mumadziwa kupemphera ndi anthu, dzaikenji manja pa iwo, bwerani tsopano. Awa ndi—apo ayikidwa mmanja mwanu; iwo ndi zikho za Mawu. Kodi inu simubwera tsopano nthawi ino, antchito anu, ndi kudzapanga njira yanu yobwerera, ife tisanasinthe msonkhano pano kwa miniti yokha. Bwerani tsopano, dzaloweni mkati. Izo nzabwino. Bwererani mchipindamo, muli malo ambiri kumbuyo uko tsopano. Mubwerere kumbuyoko ndipo mukachite zonse zomwe inu mungathe kuti muwathandize anthu okonedwa awa. Kumeneko, Yesu wawabweretsa iwo; Iye wawakokera iwo mu khoka la Uthenga. Tsopano inu muwatengere iwo kumbuyo uko ndipo tiyeni ife tipemphere limodzi nawo, kuti Mulungu amudzadze mmodzi aliyense wa iwo ndi Mzimu Woyera. Tsekani zitseko, mukhale pomwepo mpaka izo zitachitika. Iye analonjeza kuti Iwo ukanadzachita izo. Ndipo Iye analonjeza zimenezo, ndipo Iye adzasunga lonjezo Lake. Iye ndi woona basi ku lonjezo Lake, monga kuti awonekere pano pamaso pathu.

Ambuye, adalitseni iwo!

³²⁰ Atumiki, kodi muli pano? Alaliki, anthu wamba, amene ali ndi chidwi ndi kupenyera kapena kuwatenga anthu kuti alandire Mzimu Woyera, malo anu a ntchito tsopano, pitani nawo iwo, mukaime ndi anthu anu, inu amuna ophunzitsidwa bwino muli ndi Mzimu Woyera; ndipo inu akazi ophunzitsidwa bwino amene mukudziwa chimene izo zikutanthauza, inu mukhale ndi alongo amenewo kumbuyo uko kumene iwo ali. Inu amene mukudziwa choti muchite, kakhaleni nawo iwo kumbuyo uko tsopano. Pakali pano ndiyo nthawi ya inu. Apa ndi pamene malo anu a ntchito. Uwu ndi mtundu wanu, tsopano kuti muzipita. Mulungu akudalitseni inu. Uko nkulondola. Ingotangani malo anu ndi kupita mmenemo ndi iwo, ndi kukakhala pamenepo

ndi kukhala otsimikiza kuti—kuti izo zachitika, ndi kuchitidwa molondola. Kukhala pamenepo mpaka inu mutawona kukoma kwa Khristu mwa aliyense wa iwo. Mulungu adzakulemekezani inu chifukwa cha zimenezo. Amen, ndi ameni.

Oh, ine ndimakonda zimenezo. Tangwonani amene analowa kumbuyo uko!

³²¹ Kodi alipo mmodzi wina muno yemwe sanalowemo, amene ayenera kulowamo? Ngati alipo, kodi inu mungadzuke ndikuwatsatira antchito othandizira awa kukalowa mkatimo? Chitani zimenezo, mutero inu? Ngati alipo mmodzi muno yemwe—yemwe sakumverera kuti—kuti muli basi pamene inu muyenera kukhala.

³²² Tsopano, kumbukirani, m'bale, mlongo, ine—ine sindingakhoze kuzipangitsa izi kuchitika. Mwaona, Mulungu ndi Mmodzi Yemwe amachita zinthu izi, osati ine. Tsopano ine ndikupemphera kuti Mulungu angopereka zinthu izi kwa inu, ndi kukupatsani inu a—a—chokuchitikirani cha ubatizo wa Mzimu Woyera.

³²³ Anthu nonse inu tsopano amene mukuwakonda Ambuye Yesu, ndipo mukufuna kuti mukalowe mkatimo ndi kukapemphera, kubwerera kuno tsopano ndi kukapemphera ndi anthu awa. Kodi inu mutero? Zikomo inu. Zikomo inu, mokoma mtima kwambiri.

³²⁴ Inu mukudziwa, pamene ine ndiwawona antchito othandizira akupita ndi anthu, ine ndimakhala... Ine ndikufuna kuti ndinene izi za inu anthu pano, zimenezo zimatsimikizira chimene inu munapangidwa nacho. Ine ndapitapo ku malo, ngakhale, ndi anthu amene akuyenera kukhala anthu odzazidwa-Mzimu, ndi kuwona kuyitanira paguwa kukupangidwa, ndipo, bwani, iwe sungakhoze kuwatenga anthu kuti akalowe mmenemo ndi aliyense, kuti akapemphere nawo iwo. Mwaona, zimenezo zingasonyeza kuti ndi *Ichabodi*, “Mzimu wa Ambuye wachokapo.” Mukuona? Koma pamene iwe uwona changu chimenecho ndi Moto ndi kulakalaka, ndi kulakalaka miyoyo ya anthu!

³²⁵ Inu mukuzindikira, kudutsa sabatayi, ine ndinangotenga nthawi yanga, ndi kupenyereza kuzindikira za mumtima ndi zinthu monga zimenezo, kuti anthu azigwire izo ndi kupeza kuti Mzimu Woyera uli pafupi, ndiye nkupanga kuitanira kuguwa kumeneko. Azitumiki inu mukumvetsa zimene ine ndinali kuchita? Mwaona, kupanga kuitanira paguwa tsopano pamene iwo akhutitsidwa, tsopano mahandiredi a iwo ali mmenemo tsopano kuti alandire Mzimu Woyera. Ndipo ambiri analowa mmenemo ndi iwo, kukapemphera ndi iwo.

Tsopano ngati pali wina aliyense pano, kuchitira kuti. . .

³²⁶ Ine ndinena izi, kuti inu mwawona Kukhalapo kwa Khristu, sabata ino, akudzitsimikizira Yekha apa. Inu mwamuwona Iye.

³²⁷ Ndipo tsopano kumbukirani, kuti, palibe magari ati adzakhale pa ine pa Tsiku limenelo, ngati liri mawa. Izo zidzakhala, limodzi la masiku awa. Ingokumbukirani, ife tidzakayima Pamenepo. Ziribe kanthu yemwe inu muli, inu mudzakaima Pamenepo, mulimonse. “Kunaikidwa kamodzi kwa munthu kufa, ndipo pambuyo pake Chiweruzo,” ndipo ife tidzakaima Pamenepo.

³²⁸ Tsopano ngati inu simuli wotsimikiza mwangwiro kuti inu muli naye Khristu, Mzimu Woyera mu mtima mwanu, ndipo Iye akudzitsimikizira Yekha mmenemo, ndi chikondi ndi mtendere ndi chisangalalo ndi zipatso za Mzimu, ndipo Moyo wa Khristu ukukhala mwa inu, ndiye, kumbukirani, magari anu sali mmanja mwanga. Komanso Iye sadzakhala wolakwa, chifukwa Iye wawonekera pamaso panu, ndipo wadziwonetsera Yekha apa ndendende ndi Malemba. Ndi angati achitire umboni zimenezo, pokweza mmwamba dzanja lanu, ndikuti, “Ine ndaziwona Izo sabata ino”? Ndiko kulondola, mwaona, ndiye ndife opanda cholakwika. Ndife opanda chowiringula.

³²⁹ Tsopano kodi alipo aliyense akufuna, mmodzi wina yemwe angafune kuti abwere? Koterokuti ine ndikhoza kunena, monga pamene nthawi yanga ikukonzekera kuti ndizichoka pano mawa, ngati Ambuye alola, ine ndikhoza kunena kuti, “Ndine mfulu ku magari onse ku chitsitsimutso chimenecho. Ine ndinachita mwakukhoza kwanga kwenikweni, Ambuye. Ine ndikuzipereka izo kwa Inu. Tsopano Inu basi...mmodzi aliyense.”

³³⁰ Tsopano ndi angati muno, amene akudwala ndi osowa tsopano, ndipo mukufuna kuti mukhale ndi pemphero la inueni, tiyeni tiwone inu mukukwezera mmwamba manja anu. Chabwino, paliponse mchiphindachi.

³³¹ Tsopano ine ndikufunsani inu kuti mundichitire ine chinachake. Tsopano kodi ndinu okhulupirira? Tsopano ine ndikufuna inu mundichitire ine chinachake tsopano. Ikani manja anu pa wina ndi mzake. Ingoikani manja anu pa wina ndi mzake, ndipo tsopano, penyani, ine ndikufuna inu kuti mupemphere, muzingopemphera.

³³² Tsopano kumbukirani, anthu onse amene ati adzabwere mu mzere wa pemphero mawa, ayenera adzakhale pano molawirira, ndi kudzakhala ndi khadi la pemphero. Mudzaligwire ilo mmanja mwanu pamen idzafike nthawi ya mzere tsopano. Ngati inu muli naye wokondedwa, inu abale Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, aliyense yemwe inu muli, ngati inu muli nawo odwala, amene, inu—inu mubwere nawo kumene iwo, dzabwereni kumene mu mzere ndi iwo. Mudzabwere kudzatenga inu khadi la pemphero, chifukwa...Ndiye mudzabweretse khadi la pemphero mu mzere momwe; othandizira adzalitenga ilo. Iwo adzabwera pamenepo ndi kudzapempheredwa.

³³³ Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu adzachita zinthu zina zazikulu mawa. Ine ndikuyembekeza Iye ali. Ndi chifukwa chake ine ndimayitanira kuguwa, kuchita chirichonse chimene ine ndingathe, kuti ndipeze kukondedwa ndi Iye.


³³⁴ Tsopano pamene ife tonse tikuweramitsa mitu yathu, ndipo inu nonse mukupemphererana wina ndi mzake. Tsopano Baibulo linati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Tsopano inu mumupempherere mwamuna kapena mkazi yemwe inu mwayikapo dzanja lanu, pakuti iwo akukupemphererani inu. Mukuona? Musadzipempherere nokha. Muwapempherere iwo. Ikani manja anu pa wina ndi mzake, ndipo mupemphere. Ingoikani manja anu. Ndiko kulondola.

³³⁵ Tsopano mupemphere momwe inu mumachitira mu mpingo wanu. Nenani, “Ambuye Yesu, mchiritseni wosawuka uyu, wokondedwa, mlongo; wosawuka uyu, wokondedwa, m’bale; aliyense amene angakhale. Iwo akudwala, Ambuye. Ndipo ine—ndine wokhulupirira, ndipo ine nditsatira Mawu Anu. Ndipo Mawu Anu anati, ‘Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachira.’ Ndipo ine ndikusanjika manja anga pa odwala, munthu wodwala uyu, m’bale wodwala uyu, mlongo wodwala uyu. Ine—ine—ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mutsimikizire Mawu Anu, ndipo chizindikiro chitsatira, ndipo iwo achiritsidwa.”

³³⁶ Ambuye Yesu, ine ndikuwapempherera iwo, ndi mipango iyi; kuti, mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, kuti Inu muchiritse munthu aliyense yemwe ali mu Kukhalapo Kwauzimu.

³³⁷ Satana, iwe walephera nkondoyi. Iwo awona Kukhalapo kwa Khristu. Iwo awamva Mawu Ake, anawawona Iwo akuwonetseredwa. Ochimwa ali mmenemo, akufunafuna chipulumutso. Iwe walephera nkondoyi. Tuluka mwa anthu awa, mu Dzina la Yesu Khristu. Asiyeyo iwo, kuti iwe usawazuzenso iwo.

³³⁸ Ndipo mulole Mulungu wa Kumwamba awadzutsire iwo, ku moyo kachiwiri, ndi thanzi labwino ndi mphamvu. Mulole iwo amene ali ndi makadi a pemphero asadzachite kubwera nkomwe mu mzere wa pemphero, mawa. Mulole Mzimu Woyera unogogunda gulu ili la anthu, ndi kuchiza aliyense wa iwo kwa ulemelero wa Mulungu.

Tsopano pitirirani, m’bale. 

64-0404 Yehova-Yire #3
4-H Club Barn
Louisville, Mississippi U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org